

UTUMIKI WANGA WATSOPANO



Chabwino, M'bale Neville. Zikomo inu, abale.

² Moni, abwenzi. Ndithudi ndi chamwayi kukhala pano mmawa uno, mu kachisi. Pamene. . .

³ Ife tadzazana kale tsopano, ndipo tikuyembekezera msonkhano waukulu kuti uyambike mu San Jose, sabata ino, mu—mu San Jose, California. Ife tichoka mwamsanga ukatha msonkhano, waku Gombe la Kumadzulo. Ndiyeno ife tidzakhala tiri uko ku Coconut Gardens kwa pafupifupi masiku awiri, aponso, Ambuye akalola, ndi Amuna Amalonda Achikhristu. Ndipo ife tikuyembekeza nthawi yopambana mwa Ambuye, ku Gombe la Kumadzulo. Iwo ali ndi mipingo eyite-thuu imene akuithandiza, ndi magulu awiri onse oyanjana nawo aku San Joaquin, ndi zigwa kudutsa mu Gombe la Kumadzulo. Ndipo chotero ife tikakhala ku fairgrounds kumeneko. Ngati ena a abwenzi anu, inu mukudziwa, amene angafune kudzakhala nawo pa ina ya misonkhano, ife tidzakhala okondwa kukumana ndi abwenzi anu ndi—ndi abale anu.

⁴ Ndipo ife tikuyembekezera. Ine ndiri ndi kufufuza kwakukulu. . .kuyembekezera, mmawa uno, ndipo pafupifupi msonkhano uliwonse umene ine ndinayamba ndakhalapo nawo, panobe. Chifukwa, ine ndikukhulupirira kuti ife tiri basi pa usiku wa chinachake chimene chikukonzekera kuti chichitike. Ine ndayembekezera kwa icho kwa nthawi yayitali. Ndipo ine—ine ndikukhulupirira kuti ife tiri kumene kumapeto kwa izo tsopano, kwa chinachake, chimene Mulungu ati awathandizire ana Ake kupita patsogolo pang'ono pa msewu.

⁵ Inu mukudziwa, Baibulo linanena, kuti, “Pamene mdani abwera mkati ngati chigumula, Mzimu wa Mulungu umakhoza kudzutsa muyezo motsutsa izo.”

⁶ Ndipo pamene Mulungu awupatsa Mpingo Wake mdalitso, ndipo iwo amasunthira motsatira mdalitso umenewo motalika kwambiri mpaka Iwo umadzakhala wawamba kwa dziko lapansi, ndiye iwo amayamba kuwunyoza Iwo. Ndiye Mzimu wa Mulungu umabweramo ndipo umadzadzutsa muyezo kachiwiri, ndipo pali kufalikira kwa chitsitsimutso kapena chinachake.

⁷ Ndipo ziyembekezo zathu zazikulu ndi izi, kuti, limodzi la masiku awa, Mzimu wa Mulungu udzatumizanso Yesu Khristu ku dziko lapansi, ndiye izo zidzakhala zangwiro pamenepo. Umenewo udzakhala muyeso weniweni.

⁸ Tsopano iwo angoimirira, pozungulira—makoma ndi zinthu, ndi paliponse mchipindachi. Ine ndinakumana ndi munthu akubwera, pamene ndimaimika galimoto yanga, ndipo iye

anati. . . Ine ndinati, “Ine ndiyisiya iyo ikhale apa, ndi kiya, ndiye inu mukhoza kuisunthapo nthawi iliyonse imene inu mukufuna kutero.”

⁹ Iye anati, “Chabwino, ine ndinayesetsa kuti ndilowe mkati. Ine sindinathe kupeza malo oti ndiyimepo.”

¹⁰ Ndipo tchalitchi chathu ndi chaching’ono kwambiri kwa msonkhano. Koma pochoka mmawa uno. . . Ndipo ife tinalengeza izo Lamlungu lapitali, za kudzakhala pano, ndipo tikanadzabwera kuti tidzawapempherera odwala. Ndipo kuti ndidzakupatseni inu malangizo pa zomwe ife tinali titangoziwona zikuchitika. Ndipo pakhala pali zambiri, mwa chisomo cha Mulungu, zawonjezedwa kwa izo, kwa mmawa uno.

¹¹ Tsopano, ife talalikira, ndipo ena patsogolo pathu, za Kubwera kwa pafupi kwa Ambuye, Kubwera kwa posachedwepa. Ndipo ife tikukhulupirira kuti Iko kukukula moyandikirira. Ndithudi, Iko kukumakhala, tsiku ndi tsiku. Koma ngati ife tingaime ndi kuganiza, kuti, limodzi la masiku awa, inu mudzazimva izo nthawi yotsiriza, ndiyeno Ambuye Yesu adzabwera.

¹² Dziko lapansi lonse, mitengo, chirengedwe chonse, anthu, Mpingo, chirichonse, chikubuula, kulira, kugwiritsitsa, kuyembekezera tsiku limenelo, la Kudza Kwake. Chirengedwe chimadziwa kuti icho chidzatero—icho chidzasiya kuvutika pamenepo. Ndipo anthu amadziwa kuti adzasiya kuvutika pamenepo. Imfa idzataya kugwira kwake kotsiriza, ndipo manda ndi hade zidzamezedwa mu chigonjetso.

¹³ Ine ndinali wokondwa kwambiri, mmawa uno, kukumana ndi m’busa wamng’ono uyu pano amene amatiimbira ife nyimbo ndipo anaimba, wochokera ku Sellersburg. Mmodzi wa abale akhala akuyankhula za chitsitsimutso chikuchitika kumeneko. Ndipo ine ndikuganiza iwo alengeza kale zimenezo, ndi zina zotero, chotero izo nzabwino kwambiri. Ambuye awadalitse iwo pamwamba apo, mu kuyesetsa kulikonse kumene iwo akuyikapo, ndiro pemphero langa lodzipereka, kwa Ufumu wa Mulungu.

¹⁴ Tsopano, Mawu a Ambuye ndi ofunikira kwambiri kwa ife. Ife tikudziwa zimenezo. Chotero, lero, ine ndikukhulupirira kuti ife tiri pafupi kwambiri ndi Kudza kwa Ambuye, ndipo minda ndi yosowa kwambiri.

¹⁵ Ine ndakhala ndikungoyankhula ndi ena a abale. Ine ndikukhulupirira gawo lalikulu la utumiki wanga lidzakonzedwa kutsidya kwa nyanja tsopano. Ife tikukonzekera pa Afrika, ikangotha Khristimasi kumene, ndi mpaka ku Australia ndi ambiri a malowo. Ambuye akuyenda tsopano ndipo akutsegula njira kwa ife. Ife takhala tiri nako kuyitanidwa, kuzungulira dziko, kwa nthawi yaitali. Ndipo ife tikhoza

kutenga izo ikangotha Khrisimasi tsopano, ngati inu nonse muti mutipempherere ife.

¹⁶ Tsopano ine ndiri nawo pano patsogolo panga Mawu a Mulungu ali chitsegulire. Tsopano ine ndatsegula masamba, chifukwa, mwathupi, ndi mwa kuthandiza kwa Mulungu, ndine wokhoza kuchita zimenezo, kuti nditsegule Baibulo. Koma ine sindine wokhoza kutsegula zamkatizo. Alipo Mmodzi yekha Yemwe angakhoze kuchita zimenezo, ndipo ameneyo ndi Mulungu, yekha. Iye anali Mmodzi Amene analemba Iwo, mwa Mzimu Woyera Wake, ndipo Iye ndi Mmodzi yekhayo amene angakhoze kutsegula Baibulo kwa ife. Ndipo ine ndikudalira kuti Iye atsegula mitima yathu pamene ife tikuwerenga Iwo, ndipo awadziwitsa Iwo kwa ife.

¹⁷ Ine ndingokhala mwachidule, mmawa uno. Choyamba, ine ndikufuna ndichite monga ndinalonjeza kuchita, kuti ndikuuzeni inu zonse zomwe zangochitika kumene masiku angapo apitawa, zokhudza kusintha kwa utumiki wanga. Ndiyeno, ine ndiri ndi mutu wawufupi, kenako tipempherera odwala. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti pakhala ubatizo, chifukwa ine ndawona dziwe adzadzamo madzi.

¹⁸ Koma ife tisanapitirire patsogolo, tiyeni tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe tsopano mu pemphero. Ndipo ndikudabwa, ndi anthu angati muno amene akudziwa kuti inu mukumusowa Mulungu, ndipo mungakwezere mmwamba manja anu kwa Mulungu? Ndi kuti, zochuluka kwambiri pochita zimenezo, “Mundikumbukire ine, Ambuye. Ine ndikusowa zinthu zakuti-ndi-zakuti.”

Tiyeni tipemphere.

¹⁹ O Ambuye, mwakachetechete, ife tikuzindikira kuti ife tiyenera kubwera mwakachetechete mu Kukhalapo kwa Mulungu. “Pakuti iye amene abwera kwa Mulungu ayenera kukhulupirira kuti Iye ali, ndi wopereka mphotho kwa iwo amene amufuna Iye modzipereka.” Ndipo ife tikubwera mu kachetechete wa Mzimu, ku Mpandowachifumu Wanu, O Mulungu. Ndipo ife tikukwezera mmwamba mitima yathu pamaso Panu, ndikuti, “Ifufuzeni iyo, O Ambuye.” Ndipo ngati pangakhale chinthu chosayera chirichonse mwa ife, chichotseni icho, Ambuye, monga momwe Kummawa kuliri kuchokera Kumadzulo. Ndipo ngati pangakhale mphulupulu iliyonse mmitima mwathu, chinachake chimene chingatchinge mapemphero athu kuti asayankhidwe, ife tikupemphera kuti Inu mulole Magazi a Ambuye Yesu achotse banga lililonse kwa mzimu wathu ndi mtima wathu. Pakuti kunalembedwa, “Ngati ine ndisunga kusaeruzika mu mtima mwanga, Ambuye sadzandimva ine.” Ndipo Inu munawona manja pamene iwo anali kukwera mmwamba, kuti, ku maso athu athupi, akuimira

chosowa cha mitima yawo. Ife tikupemphera, O Ambuye, kuti Inu mumuyankhe mmodzi aliyense wa iwo. Alipo ambiri osowa.

²⁰ Ndipo ife tikupempha, mu msonkhano wa anthu mmawa uno, kuti Inu mukumbukire msonkhano waku San Jose uwu umene ukubwera. Tithandizeni ife, O Ambuye, pamene mahandiredi a mailosi a chisanu ndi chisanu ziri patsogolo pathu, kuti tikayendemo. Koma ife tikupita mu Dzina la Ambuye, kuti tikayesetse kuchita zonse zomwe ziri mkati mwathu, kuti tikawathandizire anthu Anu, Ambuye, muthandize otayika kuti akupezeni Inu ngati Mpulumutsi wawo, ndi kuthandiza ofooka ndi akhungu, ndi kukonza njira kwa ena amene atitsatire ife.

²¹ Mudalitse mpingo wathu wawung'ono ndi m'busa wake, M'bale wathu Neville, matrasti onse, madikoni, ndi anthu wamba, ndi aphunzitsi onse, ndi onse amene amayanjana nafe. Osati zokhazo ayi, koma mipingo yonse imene ikuimiridwa pano. Kwa anyamata awo amene akugwiritsitsa ku Sellersburg, ife tikupempha, Ambuye, kuti dzanja Lanu litambasulire kwa iwo, Ambuye. Inu muwukitse Mpingo wamphamvu wa Mulungu wamoyo, mu Sellersburg. Perekani izi, Ambuye.

²² Muwachiritse odwala, mupereke kupenya kwa akhungu, mphamvu kwa ofooka, ndi chipulumutso kwa osowa.

²³ Pamene ife tikuwerenga Mawu Anu, mmawa uno, mulole Mzimu Woyera ubwere, udzalowe mu Mawu ndi kuwafulumizitsira Iwo ku mitima yathu.

²⁴ Muwadalitse iwo amene ali oti abatizidwe. Mulole iwo adzadzidwe ndi Mzimu Woyera, pamene aziwuka kuchokera mmadzi, akupereka ulemelero kwa Mulungu. Dzitengereni ulemelero kwa Inumwini, Ambuye.

²⁵ Ndipo pamene ife tasonkhana, mmawa uno, chifukwa cha kuyeretsa kwa miyoyo yathu ndi maganizo athu, mulole ife tichoke pa kachisi uyu, mmawa uno, ndi kulimbikira kochuluka kuposa momwe ife tinayamba takhalira nako, kuti tikakutumikireni Inu. Mulole ife tikakhale moyo, titasonkhana limodzi, olukana mothinana ndi omangidwa ndi Mzimu Woyera, kufikira tsiku limenelo pamene ife tidzakumane mu Nyumba Yanu mu Ulemelero, kuzungulira Mpandowachifumu Wanu, kumene mamillioni adzakhala akuimba, "Hosanna! Hosanna!" Mulole ife tonse tidzakakhale Kumeneko, popanda mmodzi wojomba. Perekani izi, Ambuye. Kufikira nthawi imeneyo, tisungeni ife athanzi, okondwa, ndipo odzazidwa ndi Mzimu Wanu, tikutumikira Inu. Zinthu izi ife tikuzipempha mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁶ Ambuye awonjezere madalitso, pamene ife tikuwerenga tsopano mu Bukhu la Marko Woyera, mutu wa 11, kuyambira ndi ndime ya 1. Ndiyeno chitatha chobwereza chaching'ono ichi,

kapena chirimbikitso, ndiye ine ndipita ku mutu wathu. Uku ndi kuwerenga kwa chimene ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu.

Ndipo pamene iwo anabwera . . .

²⁷ Ine ndikupempha kukhululukira kwanu. Ine ndikufuna kuti ndiyambire pa ndime ya 10, kuti ndisunge nthawi, ndime ya 10 ya mutu wa 11.

Wodala ukhale ufumu wa atate athu Davide, umene umabwera mu dzina la Ambuye: Hosana mmwambamwamba.

Ndipo Yesu analowa mu Yerusalemu, ndipo mu kachisi: ndipo pamene iye anayang'ana pozungulira pa zinthu zonse, ndipo tsopano . . . madzulo anafika, ndipo iye anapita ku Bethany ndi thwelovu ake.

Ndipo tsiku lotsatira, pamene iwo anafika ku Bethany, iye anali ndi njala:

Ndipo powona mtengo wa mkuyu patali, uli ndi masamba, iye anabwera, ngati mwamwayi iye akanapeza chirichonse pamenepo: ndipo pamene iye anabwera kwa iwo, iye sanapeze kalikonse koma masamba; pakuti nthawi ya mkuyu inali isanafike.

. . . Yesu anayankha ndipo anati kwa iwo, Palibe munthu adzadye chipatso cha iwe kuyambira pano mpakana. Ndipo ophunzira ake anamva izo.

Ndipo iwo anabwera ku Yerusalemu: ndipo Yesu anapita mu kachisi, ndipo anayamba kuwatulutsa iwo amene ankagulitsa ndi kugula mu kachisi, ndipo anagudubuza magome a osintha ndalama, ndi mipando ya iwo amene amagulitsa nkhunda;

Ndipo sanalole kuti munthu aliyense anyamule chotengera chirichonse kudutsa mu kachisi yense.

Ndipo iye anaphunzitsa, kunena kwa iwo, Izo ziri . . . Kodi sizinalembedwe, nyumba Yanga idzatchedwa ya mafuko onse nyumba ya pemphero? koma inu mwaipanga iyo kukhala phanga la mbava.

Ndipo alembi ndi akulu ansembe anamva ichi, ndipo anasinkhasinkha mmene iwo akanamuwonongera iye: pakuti iwo ankamuwopa iye, chifukwa onse . . . anthu anali wodabwitsidwa pa chiphunzitso chake.

Ndipo pamene madzulo anafika, iye anatuluka mu mzindawo.

Ndipo mmawa, pamene iwo ankadutsa, iwo anawona mtengo wa mkuyu utauma kuyambira ku mizu.

Ndipo Petro pokumbukira ananena kwa iye, Mbuye, taonani, mtengo wa mkuyu umene inu munawutemberera, iwo wafota wonse.

...Yesu poyankha anati kwa iwo, Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu.

Pakuti indetu Ine ndinena kwa inu, Kuti aliyense amene adzanena kwa phiri ili, Suntha iwe, ndipo ukadziponye iwe mnyanja; ndipo nkusakaika mu mtima mwake, koma adzakhulupirira kuti zinthu izo zimene iye wazinena zichitika; iye adzakhala ndi chirichonse chimene iye wachinenacho.

Chifukwa chake Ine ndinena kwa inu, Zinthu zonse zimene inu muzikhumba, pamene inu mupemphera, mukhulupirire kuti inu mwazilandira izo, ndipo inu mudzakhala nazo izo.

²⁸ Ndi lonjezo lachisomo bwanji! Ndipo izo mwamtheradi ndi Choonadi. Ichi chinandiphunthwitsa ine, kapena momwe ine ndingagwiritsire ntchito mawuwo, kwa nthawi yayitali. “Zingakhale bwanji zimenezo?”

²⁹ Ndipo nthawi ina, pamene ine ndinkayamba kulalikira kuno ku kachisi, zaka zambiri zapitazo, ine ndinapezana ndi mawu akuti *gehena*. Ndipo ndimayendetsa cholozera kwa izo, nthawi zambiri, ndipo zimalozera ku *hade*, mu Chigriki, zomwe zimatanthauza, “manda.” Ndipo ine sindimadziwa choti ndinene, chifukwa sindikufuna kuti ndidzakhale woyankhira pa miyoyo ya anthu pa Tsiku la Chiweruzo. Chotero ine ndinafufuza izo, ndipo ndinafufuza, mpaka ine nditapeza chimene chinali Choonadi. Kwa pafupifupi zaka foro kapena faivi, ine sindimakhoza kukhudza phunziro la *gehena*, mpaka nditadzapeza chimene chinali Choonadi cha izo.

³⁰ Ndiyeno Lemba ili linandipunthwitsa ine, ngakhale mochuluka, chifukwa chakuti linali lapadera, lonjezo loterolo kukhala kuti linaperekedwa ndi Yesu Kristu. Ndipo pamene Iye ananena kwa ophunzira Ake, “Zinthu zonse zimene inu munganene, inu mukhoza kukhala nazo. Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Uzulidwe ndi kusamutsidwira kukalowa mu nyanja,’ ndipo osakayikira mu mtima mwanu, koma mudzakhulupirira kuti chimene mwanenacho chidzachitika, inu mukhoza kukhala nacho chimene inu mwanena.” Oh, ngati tingakhoze kuwayeza Mawu amenewo! “Iwe ukhoza kukhala nacho chimene *iwe* wanena. Osati chimene ine ndikunena, koma chimene *iwe* wanena. Iwe ukhoza kukhala nacho chimene *iwe* wanena.”

³¹ Kwa zaka, ine ndinakhala ndikusinkhasinkha pa zimenezo. Ine ndinapita ku lex iliyonse ndi ndemanga, kumasulira kulikonse, ngakhale ku Douay version. Ndipo womasulira aliyense amamasulira izo mofanana, “Inu mukhoza kukhala nazo zomwe inu mwanenazo.” Chotero, ine ndikudziwa kuti, ngati izo zinalembedwa mu Lemba. Kwa ine, Lemba lonse ndi

Choonadi. Ndipo ngati ine sindingakhoze kuchigawaniza Icho molondola, Icho chikadali Choonadi.

³² Chotero ine ndikukhulupirira, nthawizina, kuti Mulungu amangotilola ife kuti tiwone zinthu pamene ili nthawi yoti ife tiziwone zinthuzo. Iye amawagwira madalitso awa. Monga madalitso amene ife tikusangalala nawo lero, makolo athu akale sankasangalala nawo iwo. Ngati siyinali nyengo ya iwo.

³³ Ine ndikhoza kukumbukira pamene Mzimu Woyera... usiku umenewo pamene ine ndinabwerera ku desiki yomweyi, ndikuchokera ku mill, kumene ndinakhala ndikupempherako. Ndipo ndinakuuzani ambiri a anthu inu mwakhala pano, kuti Iye anandilamulira ine, mwa Mzimu Wake, kutuma kwa ku dziko lonse, kuti, “Opunduka adzayenda, ndipo akhungu adzapenya, ndipo mafumu ndi atsogoleri adzakhala akuitanira pemphero. Ndipo izo zidzayambitsa chitsitsimutso pakati pa abale, chimene chidzasese kuzungulira dziko, kusanafike Kudza kwa Ambuye.”

³⁴ Izo zinali zovuta kukhulupirira zimenezo. Izo zinali zovuta kuti ine ndizikhulupirire izo. Koma ndicho chimene chachitika. Izo zimangochita chinthu chimenecho. Mpaka, lero, moto wa chitsitsimutso cha Mzimu Woyera ukuyaka, kuzungulira dziko: India, Afrika, Asia, onse mpaka ku Ulaya, ndi kulikonseko. Amuna a Mzimu Woyera, odzazidwa ndi Mzimu, akuyatsa dziko lapansi, ndi chitsitsimutso cha Mphamvu ya Khristu wowukitsidwa; opuwala akuyenda, akhungu akupenya, osamva akumva, osayankhula akuyankhula. Mitundu yonse ya zozizwitsa zodabwitsa zikuchitika, chifukwa Mulungu analonjeza izo. Ndipo lonjezo la Mulungu ndi loona.

³⁵ Ndipo pamene ine ndinayamba kusinkhasinkha pa izi, ine sindikanakhoza koma kumufunsa Iye Yemwe anali kuyankhula kwa ine, “Ine ndinali wosakwanira.” Ine ndikuganiza Mulungu anayenera kusankha munthu wamng’ono, wosakhudzidwa, wosaphunzira, chifukwa, mmenemo, Iye, Mulungu, amatenga chinachake chimene sichiri kanthu, chinachake chimene chatulutsidwa kunja.

³⁶ Ndicho chimene chimandipangitsa ine kuwakonda anthu a Mulungu chomwecho. Iwo amawatulutsa iwo kunja, ngati “oyera-odzigidubuzza, kapena anthu apathengo.” Koma ndi pamene Mulungu amakhala wokonzeka kuti awatenge iwo kenako ndi kuchita nawo iwo chinachake. Ndipo icho chimamusangalatsa Iye. Izo zikusonyeza kuti Iye ndi Mulungu, samatenga kanthu ndi kupanga chinachake kuchokera mwa icho. Amamutenga wochimwa monga ine, ndi kumupanga Mkhristu; dzanja la Mulungu.

³⁷ Ine ndinamufunsa Iye za kukhoza. Ndipo Iye anandiuza ine kuti ine ndinali woti ndiziwapempherera anthu odwala. Ndipo kutumako kunali, “Uwapangitse anthu kuti azikukhulupirira ndi kukhala owona mtima, ndiye palibe chimene chidzaima ndi

pempherolo.” Ambiri a inu pano mukukumbukira zimenezo. Izo zinasindikizidwa mu zowerenga, kudutsa mdziko.

³⁸ Ine ndinafunsa, “Ine ndikachita motani zimenezo pamene ndinalibe maphunziro?”

³⁹ Iye anati, “Padzakhala zizindikiro ziwiri zidzaperekedwe kwa iwe, monga zinaperekedwa kwa Mose. Ndipo chimodzi cha izo chidzakhala pafupifupi, monga dzanja la Mose, Iye analisandutsa ilo kuchokera ku khate kupita ku machiritso.” Ndipo—ndiyeno zomwezo zinachitika, za kuika dzanja langa pa anthu, ndiyeno momwe izo zinkadziwonetsera zokha. Ndiye Iye anati, “Iwe udzadziwa zinsinsi zomwe za mtima wawo.”

Ndipo ine—ine ndinati, “Ndi chifukwa chake ndiri pano.”

⁴⁰ Iye anati, ndiye, Iye anafotokoza Malemba kwa ine. Ndipo, oh, kuyambira nthawi imeneyo, Baibulo linadzakhala Mawu atsopano kwa ine. Ine ndinali ndi kuyang’ana kosinthika pa Iwo, mawonekedwe osinthika a Iwo. Chinachake chinachitika.

⁴¹ Ndiye, mtsogolo pang’ono, Iye anati, “Ndiye ngati udzakhale woonamtima, kukhala wodzichepetsa, kukhala kutali ndi ndalama ndi zinthu,” anati, “ndiye Iwo adzakhala akungokudalitsa iwe, ndipo udzakhala ukukwera.”

⁴² Ndi nthawi zingati zimene ife timayang’ana pa amuna amene amakwera mmaudindo aakulu, chomwecho, ndi kutenga maina apamwamba, koma nthawizina izo si zimene Mulungu amadzitcha kuti zapamwamba.

⁴³ Inu mukukumbukira pamene Yohane, pamene anabwera akulalikira? Baibulo linaneneratu, kuti, “Phiri lililonse lidzatsitsidwa pansi, ndipo malo otsika aliwonse adzakwezedwa mmwamba.” Mukuona? Ndipo pamene izo zikufika, inu mungaganize kuti izo zingakhale zikuchokera Kumwamba ndi magaleta amoto. Koma chinali chiyani icho koma munthu wosauka atavala chidutswa cha chikopa cha nkhosa atamukulunga iye, ndipo kunja pa gombe la Yorodani, akulalikira. Pa gombe la matope, osati ngakhale mu tchalitchi, koma Mulungu anazitcha izo “zazikulu.”

⁴⁴ Ndipo pamene Yesu ananena kwa ophunzira, kuti, “Palibe mmodzi wobadwa ndi mkazi wamkulu monga Yohane M’batizi.” Inu mutenge mafumu onse, ndi Davide, mneneri, ndi ulemelero Wake wonse waukulu mwa Solomoni, iwo sanamukhudze nkomwe Yohane. Ndipo, komabe, iye analibe ngakhale malo oti ayikepo mutu wake.

⁴⁵ Chotero, iwe sumasowa kuti ukhale wolemara ndi wamphamvu mdziko lino, kuti ukhale wamkulu pamaso pa Mulungu. Iwe umangoyenera kukhala wodzichepetsa mu mtima mwako. Ndipo Mulungu amachitcha chimenecho “wamkulu,” iye amene ali wamkulu mokwanira kuti akhoza kudzichepetsa yekha. Ameneyo ndiye munthu wamkulu, yemwe anga—amene

angatenge mlandu pa chirichonse, amene angadzichepetse yekha. Ndiwo ukulu.

⁴⁶ Ndiye ife tikupeza kuti, izi zimene Mulungu ananena, ndiye izo zinalengezedwa kuchokera pa guwa pano, nthawi yoyamba, Iwo unachita ndendende basi zomwe Iwo unati Iwo ukanadzachita. Apo panadza mpingo wa Chipentekoste, unagwira chitsitsimutso. Ndipo, lero, mpingo wa Chipentekoste ndi mpingo umene ukukula kwambiri mdziko lonse. Chaka chatha iwo analembeza...Izo sizikutiphatikizira ife ndi—ndi awa kuchokera ku zipembedzo...Wani milioni faivi handiredi sauzande otembenuka, chaka chathachi, chimene chinaphimba Chiprotestanti chonse, kuyikidwa pamodzi, ndi Chikatolika, nachonso. Chikatolika chokha chinali, ine ndikukhulupirira, foro handiredi ndi sevens faivi sauzande, chinachake monga choncho, owatembenuza, kuzungulira dziko. Koma Pentekoste inapita milioni faivi handiredi sauzande. Mulungu akuwukonzekeretsa Mpingo Wake.

⁴⁷ Amuna opanda maphunziro, madigiri otsika, anadzuka mu Mphamvu kudzoza kwa Mzimu, amapita kunja wopanda maphunziro aliwonse kapena chirichonse, ndi kukalalikira chuma chosafufuzika cha Khristu. Ndicho chimene chiri chachikulu pamaso pa Mulungu.

⁴⁸ Ndipo ife tikuzindikira, ndiye, kuti zinthu zonsezi zinayatsa moto, ndipo Mzimu Woyera unali woona ku Mawu Ake.

⁴⁹ Patapita pafupifupi zaka faivi za kuwagwira anthu pa dzanja, kenako usiku wina, mu Mzinda wa Mfumukazi, mu Regina, mu Canada, mwamuna anayenda kudutsa pa nsanja, ndipo pamenepo anyika moyo wake wotseguka basi monga iwo ukanakhoza kukhalira, pamaso pa Mzimu. Panali kuzindikira za mumtima, monga Iye analonjezera. Izo zakhala ziri kuzungulira dziko lapansi. Izo zasindikizidwa mu zambiri, zinenero zambiri, pafupifupi kuzungulira konsekonse mdziko, mpaka dziko lonse likudziwa za zimenezo. Kenako mdani anadzabwera mmenemo ndipo anadzaziseka izo, ndipo anati, “Izo zinali kuwerenga maganizo.” Ndipo apo panali zosanzira zinabwera kwa izo, ndi china chirichonse. Koma mkati mwa zonsezo, Mulungu anasunthira chitsogolo, chimodzimodzi basi. Mulungu anakhala woona ku lonjezo Lake lokhulupirika. Iye adzatero, nthawi iliyonseyo.

⁵⁰ Tsopano ife tikudzapeza, mtsogolo, kenako, tsiku lina ine ndinali kupita ku—kokawedza, kumusi ku Dale Hollow, ndi amuna ena, Bambo Wood ndi mchimwene wake. Ndipo iwo anali a Mboni za Yehova, ndipo anali atangotembenuka kumene ndi kubatizidwa kulowa mu Chikhulupiriro. Ndipo pamene ife tinali kuwedza, uko ku gombe...Ine ndakuuzanipo inu nkhanayi, nthawi zambiri. Kumeneko Bambo Wood anati, a Banks Wood, omwe, mmodzi wa matrasti athu kuno tsopano,

ananena za mlongo winawake wachikulire yemwe anakonda kuwadyetsa iwo chidutswa cha mkate wopangidwa kunyumba ndi batala. Iye anali wa Church of God. Ndipo anati, “Lyle,” kwa m’bale wake, “ife tiyenera tipite ndi kukamuuya iye kuti ife tinapulumsidwa.”

⁵¹ Inu mukudziwa, pali zinthu zinazake basi zimene ife tikhoza kunena, zimene zimagwirana ndi Mzimu Woyera. Basi zinthu zina zimene zimamusangalatsa Iye molondola basi, ndipo pamene ife tinena chinthu chimenecho. Ine ndikufuna kuti inu muzindikire, “Chimene iwe unena.” Ngati ife titangopeza choti tinene! Mawu ako amakuweruza iwe. Mawu ako adzakutsutsa iwe, kapena mawu ako adzakudalitsa iwe.

⁵² Ndipo, mosazindikira, Banks ayenera kuti ananena chinthu cholondola. Pakuti iye asananene kuti . . .

⁵³ Ine ndinali nditakhala kumbuyo kwa ngalawa, ndikuwedza ndi chingwe chamedza kuphera nsomba yaing’ono ya maakha a buluu kuti akhale, kuika pa mbedzapo ngati nyambo, pakuti nyambo zinali zitathira. Ndipo ine ndinali kugwira nsomba zazing’ono izi ndi kumaziya izo mu ndowa, kuzisungira mbedza.

⁵⁴ Ndipo pamene Banks ananena zimenezo, zonse mwadzidzidzi Chinachake chinandikhudza ine. Iye ananena chinthu cholondola. Ndipo Mzimu Woyera unayankhula ndipo unati, “PAKUTI ATERO AMBUYE. Iwe ukapeza, mu maora pang’ono otsatirawa, padzakhala chiukitsiro cha nyama yaing’ono.” Ine ndinaganiza uyo adzakhala mwana wa mpaka yemwe ine ndimaganiza kuti mwana wanga wamufinya mwamphamvu, ndikufinyira panja mpweya kuchoka mwa iye, ndipo—ndipo anali atamugwetsera iye pansi, ife tisanachoke. Ine ndinaganiza ndicho chimene icho chiti chidzakhale. Koma mwa kudabwitsidwa kwathu, mmawa wotsatira, pamene ife tinali titakhala mu ngalawa . . .

⁵⁵ Ine ndikudziwa Banks ali pano. Ine ndikuganiza Lyle . . . Kodi Lyle ali pano, Banks? Kapena, ngati inu muli, Lyle, kwezani mmwamba dzanja lanu. Iye amabwera kuno, amakhala nafe, nthawi zonse.

⁵⁶ Iye anali . . . anagwira nsomba, ndi imodzi . . . mbeza yaitali. Ndipo iye anagwira nsomba yaing’ono, ya makha a buluu, ndipo iyo inameza mbeza njira yonse mpaka pansi. Ndipo anaigwira nsomba yaing’ono. Mmalongochotsa mbedza kuchokera mkamwa mwake, iyo inagwidwa mwakuya kwambiri, mpaka, iye anangoikoka iyo. Ndipo iye anakoka—mmimba, ndi matumbo, ndi makha, ndi zonse, kuchokera mkamwa mwake momwe. Ndipo anangoiponyera iyo pamadzi, kansomba kakang’ono monga momwe tinali kupha nsomba, usiku watha, ndipo anali atadula handiredi za iwo, kapena kupitirirapo, kukhala nyambo. Ndipo kanthu kakang’onoko kanaphupha

kaforo kapena kafaivi, ndipo kanayesera kugwiritsa ntchito kamwa yake yaing'ono, koma iko sikanakhoze, chifukwa iko kanali katadzazidwa ndi makha ndi zina zotero. Ndipo Lyle anati, "Iwe wawombera phukusi lako lomaliza, munthu wamng'ono." Ine ndinapitirira, kumawedza, osaganizira kalikonse za izo.

⁵⁷ Ndiye, Mulungu amachita zinthu mwachilendo kwambiri. Zonse mwadzidzidzi, ine ndinamverera kuti kukubwera Chinachake, pansi pamwamba pa tchire limenelo. Mzimu Woyera unasunthira pamenepo ndipo unati, "Imirira." Unati, "Yankhula kwa nsomba yaing'ono iyo, ndipo iyo ikhalanso ndi moyo wake." Iyo inali itagona pamenepo, yakufa, kwa theka la ora, itayandama mmbuyo mu udzu.

⁵⁸ Ine ndinati, "Nsomba yaing'ono, ine ndikukupatsa iwe moyo wako, mu Dzina la Ambuye Yesu." Nsomba yaing'ono ija inatembenuka, inagudubuzika ndipo inatuluka kudutsa mmadzimo mwamphamvu momwe iyo ikanapitira. Ine ndinaima pamenepo, osadziwa choti nkuchita.

M'bale Banks Wood anati, "Ndi zabwino kuti ife tiri kuno."

⁵⁹ Ndipo Lyle anati, "Izo zimatanthauza ine, chifukwa ine ndinanena chinthu chimenecho kwa iye, 'Iwe unawombera phukusi lako lomaliza, kamunthu kakang'ono.'" Ndipo iye anatengeka yense.

⁶⁰ Ine ndinati, "Ayi, si choncho." Ine ndinali kuyesera kumutonthoza Lyle. Ine ndinati, "Izo si chomwecho."

Ndiyeno Lemba ili linabwera kwa ine kachiwiri.

⁶¹ Ine ndinali ndi pafupifupi ana handiredi aang'ono akugwa pa mndandanda, kuti ndi wapempherere, anthu ambiri ali ndi leukemia ndi khansa, ndi chifuwa chachikulu, akudyedwa, akhungu, ndi ogontha, ndi osayankhula. Kuli tsamba pambuyo pa tsamba, ku nyumba kwanga, odzaza ndi zimenezo, ndipo zikuwoneka ngati Mulungu wachifundo akanapereka izo mmalo mogwiritsa ntchito Mphamvu Yake pa nsomba yaing'onoyo, yopanda mawonekedwe.

⁶² Koma Iye akukhalabe Mulungu. Nchifukwa chiyani Iye sanagwiritse ntchito Mphamvu Yake pa akhate pa chipata, mmalo mwa mtengo wawung'ono wa mkuyu uwu? Ndi zoti zichite chiyani? Mulungu amafuna kuti asonyeze kuti Iye ndi wokhudzidwa. Iye amadziwa zinthu zonse. Iye ndi Mulungu, pa mtengo wa mkuyu. Iye ndi Mulungu, pa nsomba. Iye ndi Mulungu, pa chirengedwe. Iye ndi Mulungu, pa zinthu zonse, ndipo palibe kanthu kakang'ono kwambiri kapena kopanda mawonekedwe koma kamene Iye amasangalatsidwa nako. Kotero izo zingatipatse ife kudziwa, ngakhale kuti ndife ang'ono ndi osafunikira, Mulungu amakhala ndi chidwi mwa ife kuti tichite chinachake kwa Iye. Iye amakonda kuwonetsera Ulemelero Wake.

⁶³ Ndipo menezizo zinandikanirira ine mwampahmvu kwambiri, mwakuti ndinkalephera kuti ndipume nkomwe, usana ndi usiku. Zimenezo zakhala ziri zaka ziwiri zapitazo, ndipo mowirikiza izo zakhala zikundisautsa ine. Ndipo ndinati, “Oh, ine sindingakhoze basi kunena kanthu za izo, pakuti ine sindingakhoze kuziyika izo mu Chitetezero. ‘Chirichonse chimene *iwe* unena, icho chidzafika pochitika. Iwe ukhoza kukhala nacho chimene *iwe* wanenacho.’” Ndipo ine ndaimapo pano pa guwa lomweli, ndi kuyesetsa, ndi kumayendetsa Lemba; ndipo ndikudziletsa kwa izo, ndi kubwereranso, chifukwa ine ndinkachita mantha kuzigwiritsa ntchito zimenezo. Iwe sungakhale ndi chikhulupiriro pokhapokha utadziwa chimene ukuchita.

⁶⁴ Munthu wina anabwera kwa ine, osati kale litali, ndipo iye anati, “M’bale Branham, kodi inu mukuganiza kuti ndi zolakwika kuti Mkhristu azisuta fodya?”

⁶⁵ Ndipo ine ndinati, “Kodi inu mukundifunsiranji ine?” Ngati pali funso mmalingaliro mwanu, zisiyeni izo zokha. Musati konse...

⁶⁶ Iwe sungakhale ndi chikhulupiriro pokhapokha ngati uli wotsimikiza mwangwiro kuti iwe ukulondola. Pamene mithunzi yonse yachokapo, ndiye iwe ukhoza kukhala ndi chikhulupiriro ndi chidaliro.

⁶⁷ Ndipo ine sindingakhoze kuyenda kupita kumeneko ndi kukalalikira Lemba limenelo, osadziwa chimene ine ndinali kuchiyankhula. Komabe, ine ndinadziwa kuti izo zinali za Ambuye. Ambiri a anthu inu mundichitira ine umboni, kuti, kwa zaka ziwiri zapitazi, inu mwandimvapo ine mowirikiza, kuchokera pa nsanja iyi, ndikunena kuti pali chinachake, chinachake, penapake. Ine ndikuchifikira. Ine ndikudziwa kuti icho chayandikira. Ine sindikuwoneka basi kuti ndikuchigwira icho. Ine nkuti, “Ine ndikapezana ndi Lemba pamenepo, ine sindikumadziwa choti ndichite.”

⁶⁸ Chifukwa, Malemba, oh, iwe ukhoza kuyikapo kutanthauzira. Ngati winawake andifunsa ine, ine ndikananena chinachake kwa iwo, ndi kuchokapo, ndi kutembenuzira kwa chinachakenso. Koma kuyang’anizana ndi nkhaniyo... Chimodzimodzi monga, ife tiyenera kuyang’anizana nayo nkhaniyo, kodi ubatizo wa Mzimu Woyera ndi wolondola kapena wolakwika? Ife timayenera kuyang’anizana nayo nkhaniyo, kodi Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Kodi ndi zoonza kapena zolakwika? Ife tiyenera kuti tiziyang’anizana nazo izo. Ife tiyenera kumadziwa kuti Mawu a Mulungu nthawizonse amakhala owona.

⁶⁹ Chotero, icho chimapitirira, chokwera ndi chotsika. Ndipo ine ndimachiyika icho mmalingaliro anga, ndipo sindimakhoza basi kuchichotsa icho. Ndipo kulikonse kumene ine ndimapita,

icho chimangobwera kwa ine mowirikiza, “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili, ‘Zulidwa ndi kuponyedwa mu nyanja,’ ndipo osakaika mu mtima mwanu, koma mudzakhulupirira kuti zomwe mwanenazo zidzachitika, inu mukhoza kukhala nazo zomwe mwanenazo.”

⁷⁰ Ine ndinaganiza, “Izo zingatheke bwanji, Ambuye? Ameneyo kukhala *ine* ndikunena zimenezo. Ine nkuti... Izo zizingachite ubwino uliwonse, pakuti izo zingakhale *ine* ndikunena izo. Chotero, ine sindingakhoze kunena kanthu koma zomwe Inu mwanena. Ndipo ine—ine ndingangonena izo, mwa Malemba.”

⁷¹ Ndipo zinthu zonse zinakhazikika pa Chitetezero. Sikumakhala madalitso kunja kwa Chitetezero. Chifukwa, ndife ochimwa, kunja kwa Chitetezero. Ngati icho chikanangokhala chinthu cha konsekonse cha aliyense, ndiye aliyense akanapululumutsidwa. Koma ndi kawonedwe kako pa madalitso a Chitetezero, kamene kamabweretsa madalitso kwa iwe.

⁷² Monga chipulumutso, bola ngati zinakhudzana ndi Mulungu, ine ndinapululumutsidwa pamene Yesu anafa. Koma izo zizingandichitire ine ubwino uliwonse mpaka izo zitawululidwa kwa ine kuti Iye ndi Mwana wa Mulungu, ndipo ndamuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wanga. Ndipo Lemba lirilonse limakhala mwanjira yomweyo.

⁷³ Machiritso Auzimu ndi a iwe, ngati Mulungu angawulule izo kwa iwe, kuti izo ndi za iweyo. Koma sungati ungopunthwa pa izo. Izo ziyenera kubwera mwa vumbulutso. Ndipo pamene izo zawululidwa, kuti, “Ndi mikwingwirima Yake inu munachiritsidwa,” palibe chirichonse chimene Satana angakhoze konse kuti achite.

⁷⁴ Monga m’bale wathu wamng’ono wochokera ku Sellersburg ananena, “Adierekezi onse sangakhoze kuzisuntha izo,” ndithudi, pamene chinachake chawululidwa.

⁷⁵ Zindikirani. Ndiye, mu kugwa kotsiriza kwa masamba uku, ambiri anena kwa ine, “Nchifukwa chiyani, m’mawa uliwonse, inu, pamene inu muli kwanu, inu mumanyamula mfuti yanu ndikumapita kuthengo kukasaka?”

⁷⁶ Ine ndikufuna kuti inu mudziwe kuti Iye ndi Mulungu wa mnkhalango chimodzimidzi basi monga Iye ali Mulungu wa mu mzinda. Iye ndi Mulungu mochuluka basi kunja uko monga Iye amakhalira kuno. Ndipo Mulungu nthawizonse amachita ndi anthu molingana ndi momwe iwo aliri, ndi chiyani. Monga Davide, mmphepete mwa madzi odikha ndi msipu wobiriwira, chifukwa iye anali m’busa. Ndipo Iye ali nazo njira zosiyanasiyana, kuwulula, ndi chinachake.

⁷⁷ Ine ndimadzuka, mmawa, kupita ku nkhalango, molawirira kwenikweni, pafupifupi foro koloko, kukasaka agologolo. Ndipo mkazi wanga mpaka ananena kwa ine, iye anati, “Billy, kodi iwe sumatopa kupita kukasaka?” Mwaona, nkondo

iyi imapambanidwa, ndiwekha. Mkazi wanga samamvetsa zimenezo. Ine sindimazimvetsa izo. Koma iyo ndi nkondo. Iwe umayenera kuyima, wekha. Palibe amene angaime ndi iwe. Pamangokhala malo a iwe basi ndi Yesu. Kusamvetsetsedwa? Ndithudi.

⁷⁸ Ngakhale kwa mtsikana wanga wamng'ono apo, Rebekah. Iye anati, “Ngati ine ndingadzakwatiwe konse ndi mwamuna, ngati iye adzatchule zoti amapita kokasaka, ine sindidzakwatirana naye iye.” Anati, “Ine ndikudziwa zimene amayi anga akhala akudutsamo. Mwamuna amakhala kunja, ndipo amakhala atapita mmisonkhano; mwamsanga pamene iye wabwera kunyumba, akugwira mfuti yakale kapena mbedza ya nsomba, ndi kumapita kuthengo.”

⁷⁹ Ine ndinati, “Kodi iwe ungakonde kuti iye azichita zimenezo, kapena kodi iwe ungakonde kuti iye azigwira mpukutu wa makadi kapena—kapena la bulondi ina, ndi kumachokapo? Tsopano ungogamula lingaliro lakolako.”

⁸⁰ Pamene ine ndinabwerera tsiku limenelo, iye anati, “Adadi, ine ndikupepesa chifukwa cha zimene zija. Ine ndidzakwatiwa mwamuna monga inu, amene amakonda kusaka, ndiye ine ndizikasaka naye iye.” Iye anati, “Ine ndizidzapita kumeneko ndi iye.”

⁸¹ Ine ndinati, “Chabwino, izo nzabwino, aponso. Ine ndikanakonda iwe ukanayankhula ndi amayi ako pang'ono pokha, za zimenezo.”

⁸² Koma kumakhala chinachake mu nkhalango. Pamene ine ndinaphunzira koyamba za Mulungu, ine ndinkafuna kulapa. Ine sindinkadziwa momwe ndingalapire. Ine sindinkadziwa momwe ndingayankhulire kwa Iye. Chotero, ine ndinakhala pansi, ndipo ndinamulemba Iye kalata, ndipo ndinamufunsa Iye kuti andikhululukire ine. Ndipo ine sindimadziwa momwe ndingachitire izo. Kotero ine ndinadziwa kuti ine ndinamverera chinachake, uko mu nkhalango, ndipo ine ndinadzaikhomerera iyo pa mtengo, kotero pamene Iye adzatsike kudutsa mnkhalangomo, pa malo amene ine ndinamuwona Iye, kuti Iye adzakhoze kuwerenga iyi, ndipo adzamvetsa chimene ine ndimatanthauza, kuti ine ndinali wopepesa kuti ine sindinali kumutumikira Iye, ndipo ine ndikufuna kuti Iye andikhululukire ine tchimo langa.

⁸³ Ndiye ine ndinadzichitira ndekha manyazi, ndipo ndinaitenga iyo. Ine ndinati, “Ngati Iye ali Munthu, Iye amvetsa ngati munthu. Iye ndi Mlengi wanga.” Ndipo ine ndinafika pansi mu shedi ndi kuyamba kuyankhula ndi Iye ngati munthu, ndipo Iye anandiyankha ine mondiyankha ngati munthu. Ndiye izo zinali pa. . .

⁸⁴ Ine ndiri ndi madeti ena amene akhala pansi apa. Pa Okutobala 12...Pa 15, nyengo ya gwape inali ikutseguka,

uko mu Wyoming. Pa 12 linali tsiku lotsiriza limene ine ndikanakhoza kusaka, ndipo ife tinali oti tinyamuke pa 12. Ine ndikutanthauza, pa 10 ife tinali mu nkhalango, limene linali Loweruka. Lamlungu, ine ndinalalikira, limene linali pa 11. Lolemba, M'bale Sothmann ndi M'bale Roberson kumbuyo uko, ndi tonse a ife, ife tinanyamuka kupita ku—ku msonkhano, kapena kokasaka agwape uko mu Wyoming. Mmawa umenewo, wa 10 umene ukanati ukhale... Ndiye, pa 18, nyengoyo ikanatsekedwa mu Indiana, ife sitikanakhala ndi kusaka agologolo aponso.

⁸⁵ Chotero ine ndinati, “Iyi ikhala nthawi yotsiriza imene ine ndingapite kunja.” Ndipo ife tinasonkhanitsa gulu limodzi, ndipo ine ndinawasokeretsa iwo kuzungulira mnkhalango. Ine ndinabwerera mmbuyo kutali, mpaka ku malo kumene ine ndimakonda kupitako, ku Salemu. Nyengo inali itatha. Agologolo anali apang’ono. Ine ndinali nditatuluka kangapo, kumangopha gologolo mmodzi nthawi imodzi.

⁸⁶ Chotero, mmawa uno, ine ndinapita ku nkhalango komweko, ndipo mphepo inawuka ndipo inayamba kuwomba. Ndipo aliyense amene amasaka, amadziwa kuti zimenezo ndi mmawa woipa. Ine ndinasaka kudutsa mnkhalango yonseyo, popanda kumuwona gologolo mmodzi, kapena kumumva mmodzi. Ine ndinapita kumusi kwa mtsinje, ndipo ndinayamba mmwamba kuti ndikapeze kagawo kakang’ono ka nkhalango. Ndipo pamene ine ndimayandikira pafupi ndi nkhalango yaing’ono iyi, uko kunali—mitengo yambiri ya walnut, ndi mitengo ya dzombe, masamba onse atagwapo pa iyo, chitsamba chopanda kanthu basi. Pambali pawo panali mitengo iwiri ya mkuyu. Tsopano, agologolo samakhala pafupi ndi mikuyu. Koma kuchokera pamenepo, ine ndinawona, zinkawoneka ngati, ine ndinawona... Ine ndinamuwona gologolo akukwera kudutsa mu nkhalango, koma iye amathamanga kwambiri.

⁸⁷ “Oh,” ine ndinati, “palibe chifukwa chomusakira. Kuno kuli anthu kunja kuno, alimi akutola chimanga chawo, kuzungulira tchire laling’ono ili. Agologolo sangakhaleko kuno.” Chotero ine ndinakhala pansi pakati pa mitengo iwiri, ndipo ndinapachika miyendo yanga m’mwamba pa umodzi ndi kudzatsamira pa winayo mu kutentha kwa dzuwa, Ine ndinaganiza, “Ine ndingogona pang’ono, kenako ine ndikamutenga M'bale Banks, ndi M'bale Sothmann, ndi anyamata, pamene ine ndikubwerera, ndipo, kumatsika mu msewu.”

⁸⁸ Ndipo pamene ine ndinakhala pamenepo... [M'bale Branham akukhosomola—Mkonzi]. (Mundikhululukire ine.) Pamene ine ndinakhala pamenepo, pansi pa mtengowo, ndinangofikirira pansi, ndipo dzuwa lofunda likuwalira pa ine, *Chinachake* chinati, “Ngati iwe unena kwa phiri ili, ‘Iwe zulidwa, ndipo ukaponyedwe mnyanja,’ ndipo osakaika mu mtima mwako, koma kukhulupirira kuti zinthu zimenezo

zimene iwe wazinena zichitika, iwe ukhoza kukhala nacho chimene wachinenacho.”

⁸⁹ Ine ndinati, “Chabwino, tsopano, labweranso Lemba limenelo mmalingaliro anga kachiwiri.” Ine ndinati, “Ine ndiri ndi kanthawi kuno, pafupifupi ora ine ndisanati ndipite ndikukawatenga anyamata ena onsewo, kotero ine ndingowerenga Lemba limenelo.” Ndipo ine ndinati, “Tsopano, izo zingakhale motani?” Ndinati, “Umu ndi momwe izo ziyenera kuti zinakhallira, kuti, ophunzira amenewo ankakhala mbali inayo ya Chitetezero. Chitetezero chinadzachitika mtsogolo, pafupifupi, oh, masabata angapo mtsogolo, Chitetezero chisanapangidwe. Yesu anawapatsa iwo Mphamvu, mbali ina ya Chitetezero, monga Iye anachitira ndi aneneri.”

⁹⁰ Ndipo pamene ine ndinati, “aneneri,” Chinachake chinandikhudza ine kachiwiri. “Aneneri anali chiyani?” Ndiye ine ndinayamba kuganizira za zimenezo, za chimene Iye ankachita ndi aneneri.

⁹¹ Ndipo izo zinafika, nditatha kuyankhula pamenepo kwa kanthawi, mkati mwanga, ndikungoganizira basi, mpaka ndinazindikira kwambiri za Chinachake kuti chiri pafupi, mpaka ine ndinali kuyankhula kwa Winawake. Ndipo Chinachake chinati kwa ine, “Zimenezo ziri mu Chitetezero. Pakuti ngati mwamuna kapena mkazi adzipatula kwambiri ndi kudzipereka kwa Mulungu, kuti Mulungu amangosunthira mkati ndi kumagwiritsa ntchito liwu lawo, ndipo samakhala munthuyo akuyankhula. Ndi Mulungu yemwe ali mwa iyeyo akuyankhula.”

Ine ndinaganiza, “Izo nzoona.”

⁹² Chinachake chinanena kwa ine, “Iwe ukuganiza chiyani . . . Iwe umawawona chotani masomphenya amenewo pa nsanja? Iwe umawawona chotani masomphenya amenewo kunja kuno? Ndi chiyani chimenecho? Kodi iwe ukuganiza kuti ingakhale nzeru yako yomwe kuti iwe umakhoza kulosera chinachake chimene chimadzachitika nthawi iliyonse mpaka ku lemba? Kodi ukuganiza kuti ndi iweyo umakhala ukuyankhula? Kodi iwe ungaganize nthawiyina . . . Pamene Mzimu Woyera ulowa mu Uthenga, ndipo iwe sukudziwa choti unene, kodi ndi chiyani Icho chimene chimayankhulacho ndiye? Chimakhala chiyani pamene munthu akuyankhula ndi lirime limene iye sakudziwa kanthu za izo? Ndi chiyani chimene chimatanthauzira lirime lomwelo, popanda mmodzi wa iwo wodziwa chirichonse cha izo? Kodi ndi munthuyo payekha, kapena kodi ndi Mzimu wa Mulungu wamoyo?”

⁹³ Ine ndinati, “Izo nzoona. Ine ndikuziwona izo. Ndi Mulungu yemwe akuyankhulayo. Ndipo chonse chimene Mpingo umasowa ndi sitepe yoyandikira kwa Iye, moyo wochulukira wodziapatula, kumakhala ndi Iye.”

⁹⁴ Ndipo pamene ine ndinali nditakhala pamenepo, kwa mphindi chabe kapena ziwiri, ndikuganizira pa izi, ine ndinadzigwira ndekha ndikuyankhula ndi Winawake. Ndipo ine ndinamva Chinachake chikuti, “Pempha. Nena chimene ukuchifuna, ndipo icho chidzafika pochitika.”

⁹⁵ Ine ndinati, “Kodi Inu ndi chiyani?” Ine ndinati, “Kodi ine ndikuyankhula ndi ndani? Inu ndinu Ndani? Ndani waima apa mu tchire ili, yemwe ine ndikukhoza kumva Liwu ilo likuyankhula kwa ine? Inu ndinu Ndani? Mukuyankhula kwa ine.” Ine yense ndinatengeka ndipo ndinalumpha mmwamba kuchokera pakati pa mitengo imeneyo. Ine ndinati, “Yankhulani ndi ine. Ndinu Ndani? Ine sindikukhoza kukuwonani Inu.” Ine ndinakufunafuna Kuwala kuja pamenepo. Ine sindimakhoza kuwona kanthu. Ine ndinakuwa mokweza, “Inu ndinu Ndani? Kodi Inu muli kuti? Kodi Inu mukufuna chiyani ndi ine? Ambuye, Inu muli pati?”

⁹⁶ Chinachake chinasunthira mmbuyo, ndi kuti, “Nena zomwe iwe ukufuna ndipo izo ziperekedwa kwa iwe.”

⁹⁷ Ine ndinati, “Ambuye, kodi Inu mukusinthu utumiki wanga? Kodi uku ndi kusintha kumene Inu mwakhala mukukukamba? Kodi ichi ndi chimene iwo ukubwerako? Kodi ichi ndi chimene chiti chidzakhale? Chinachake mnyumba yaying’ono iyo chimene ine ndinachiwona mmasomphenya, kodi ichi ndi chimenecho?”

⁹⁸ Basi pomwepo kudzodza kozama kwenikweni, kokoma kwa Mzimu Woyera kunandidzutsa ine, monga, kuchokera pa mapazi anga, ndipo anati, “Nena zimene iwe ukufuna, ndipo izo ziperekedwa kwa iwe.”

⁹⁹ Ine ndinaima pamenepo, wodabwitsidwa. Izo zinandichokera ine. Ine ndinalibe kalikonse. Ine ndinaganiza, “Chabwino, kodi ine ndinganene chiyani? Palibe anthu odwala pano. Palibe kalikonse pano. Ine ndiri mu nkhalango. Kodi ndinganene chiyani? Chiyani—chiyani—kodi ndichite chiyani?” Ndipo ndinaganiza, “Kodi ine ndikupenga? Kodi ine ndawerenga kwambiri mpaka mphamvu zanga zamalingaliro zikusweka?”

¹⁰⁰ Ndipo basi pomwepo ine ndinamva Iwo, chimodzimodzi basi monga inu mukundimvera ine, anati, “Kodi iwe sukusaka, ndipo iwe ulibe nyama?” Anati, “Yankhula chirichonse chimene iwe ukuchifuna.”

¹⁰¹ Chabwino, ine ndinaganiza izi, “Mulungu anati, ‘Tsimikizirani zinthu zonse.’” Ine ndinati, “Ambuye Mulungu, ngati zimenezo muli Inu, ndipo ichi ndi chizindikiro kuti Inu mukukonzekera kuti musinthe utumiki wanga kuchokera ku masomphenya amenewo, kupita ku chinachake chokulirapo, chimene ine ndakhala ndikuchiyembekezera nthawi yaitali,” ine ndinati, “mulole icho chidzachitike kuti Inu muyankhe

pemphero langa.” Ndipo ine ndinaima pamenepo pang’ono pokha. Ndipo ndinaganiza, “Kodi Iye ananena chiyani? Iye sananene kuti, ‘Pemphera.’ Iye anati, ‘Nena chimene iwe ukufuna. Ungonena icho, ndipo mawu ako adzawonekera. Nenani kwa phiri ili, ndipo izo zichitika monga momwe iwe ukunenera.”

¹⁰² Chotero ine ndinayika phewa langa pa mtengo. Ndipo ndinazolowera...Ndinaiyika mfuti yanga pa mayadi fifite, kuti iziyendetsera zipolopolo. Chotero ine—ine ndinayang’ana pozungulira, kuti ndiwone mtengo pa mayadi fifite. Ndipo umodzi unali mayadi fifite kutalikira kwake, kunja—kunjwa kwa masamba. Ine ndinati, “Ndi pafupifupi zosatheka kwathunthu kuti gologolo abwere ku mtengo umenewo, pomwe apa, ndi alimi awo kumeneko akutola chimanga chawo.” Ine ndinati, “Koma padzakhala gologolo wofiira ati adzatuluke pa mapeto a nthambi imeneyo ndi kudzakhala pansi pamenepo, ndipo ine ndidzamuwombera iye kuchokera apa.”

¹⁰³ Ndipo ndisananene nkomwe zimenezo, apo panali gologolo. Ine ndinanjenjemera pang’ono, ndipo ndinaikhazika pansi, ndi kuwombera gologoloyo. Ndinayenda ndikukamunyamula iye. Ine ndinali kunjenjemera, paliponse.

¹⁰⁴ Ine ndinati, “Mwinamwake izo zinangochitika mwanjira imeneyo.” Inu mukudziwa momwe anthu angakaikirire. Koma iwe umafuna kuti ukhale wotsimikiza. Osachita kanthu kupatula ngati iwe watsimikiza, ndiyeno iwe umadziwa zimene ukuchita. Ine ndinasisita nkhoze yanga pang’ono, ndipo ndinayang’ana, ndinawombera diso mwangwiro. Chotero ndinakwera mmwamba ndipo ndinakakhala pansi pambali pa phiri, ndipo ndinati, “Ambuye, munalembedwa mu Mawu Anu, kuti, ‘Kamwa ya mboni ziwiri kapena zitatu, mulole mawu aliwonse akhazikitsidwe.’” Ine ndinati, “Ngati uyo munalu Inu, mundikhululukire ine pa kupusa kwanga. Koma ine ndikukupemphani Inu kuti mundipatse ine gologolo wina monga chomwecho, ndipo,” ine ndinati, “ndiye ine ndikukhulupirirani Inu, kuti Ndi Inuyo, ndipo mdierekezi sakhala ndi chipinda chirichonse chonena kuti izo zinangochitika mwanjira imeneyo.” Chotero ine ndinakhala pansi.

¹⁰⁵ Mu mphindi chabe, apa panabwera Kumeneko, ine ndimakutcha Iko, “Kudzoza kwapamwamba,” kunadzasesa kachiwiri. Ndipo ndinali pafupifupi kunyamuka pa mapazi anga. “Ndipo anati, nena chimene iwe ukufuna, ndipo icho chidzapatsidwa kwa iwe.”

¹⁰⁶ Ine ndinayang’ana kudutsa mu nkhalango mpaka ine ndinapeza mtengo wina pa mtunda wa mayadi fifite, unali ndi masamba ambiri pa iwo, ndi nthambi za mphesa ndi zinthu zitakulungidwa mozungulira, kumene agologolo samakonda kukwera mtengo woterowo. Ine ndinati, “Ndipo pakhale

gologolo wina wamng'ono wa nkhandwe atakhala pomwe apo." Ndipo ine ndinatenga chala changa pansi, ndipo ndinayang'ana pozungulira mu tchirelo.

¹⁰⁷ Ndipo ndinayang'ana mmbuyo, ndipo apo panali gologolo wa nkhandwe akuyang'ana pa ine pomwe, kachiwiri. Ine ndinamuwombera ameneyo. Ndinamunyamula iye. Ndipo ndinaganiza... Oh, ndinali ndikunjenjemera.

¹⁰⁸ Ine ndinaganiza, "Taganizani! Mulungu wamkulu wamphamvu wa Kumwamba ali kuno mu nkhalangoyi, ndipo Iye akutsimikizira kwa ine, mwanjira yanga yomwe, ndikusaka kuno, kuti Iye achita ndendende basi zimene Iye anandiuza ine zaka fikitini zapitazo." Ine ndinaziyang'ana izo pang'ono pokha. Ine ndinati, "Ambuye, izo zichitika kachiwiri."

Iye anati, "Yankhulani malo amene iye ati akhalepo."

¹⁰⁹ Ine ndinati, "Ine ndipanga chowonjeza ichi." Ine ndinati, "Chitsa chakale chikutulukira kumenekocho, kumbali ya mundawo, chopanda kanthu, choterera ndi choyera." Ine ndinati, "Pabwere gologolo wina wofiira, ndipo iye apite pamapeto a chitsa chimenecho, ndipo aziyang'ana kumunda, kwa alimi. Izo zikhale mwanjira imeneyo."

¹¹⁰ Ine ndinayang'ana mmbuyo ndipo apo panalibe gologolo pamenepo. Ine ndinayang'ana kwa pafupifupi maminiti asanu. Apo panalibee gologolo. Ine—ine ndinati, "Chabwino," ine ndinati, "awiri, agologolo awiri ndi zabwino." Ine ndinati, "Awiri ndi mboni. Ine ndikhulupirira izo monga chomwecho."

¹¹¹ Ndipo Chinachake chinati, "Koma iwe unati pakhale mmodzi." Ine ndinayembekezera maminiti ena faivi. Panalibe. Ndipo Iwo unapitirira kumabwereza mu mtima mwanga, "Iwe unati pakhale mmodzi." Ine ndinadikirira ndipo ndinadikirira. Chinachake chinati, "Kodi iwe ukukaikira?"

Ine ndinati, "Osati mpang'ono pomwe."

¹¹² Ndipo ine ndisananene konse zimenezo, mpaka nthambi imeneyo inapita gologolo wofiira, anaima ndipo anadzayang'ana pa alimiwo. Mulungu ndi woweruza wanga, nditaima pano. Ine ndinamuwombera gologoloyo, ndinapita pamenepo ndipo ndinakamunyamula iye. Ndipo ndinayenda kudutsa mnkhalangomo mpaka ine ndinali nditadutsa maora angapo ndikuwatenga anyamatawo, kuti ndiwone ngati pangakhale mmodzi winanso, paliponsepo. Ndipo apo panalibe.

Ndiye ine ndinabwera kunyumba, ndinakuuzani inu za zimenezo.

¹¹³ Ndiyeno pa Novembala 7, ine ndinali uko mu Kentucky. Ine ndinali ndi mlamu wake wa M'bale Wood, ataima pamenepo, Charlie Cox, ataima pamenepo pa nsanamira. Ndipo ndi M'bale Tony Zabel, mmodzi wa madikoni muno mu tchalitchi. Kodi inu muli pano, Tony? Iye ali pano penapake, M'bale

Tony Zabel, ndiponso M'bale Banks Woods. Ndipo ife tinali pamwamba mmapiri, tikusaka. Ndipo ine ndinayamba kupita mnkhalango, ndipo agologolo anali osowa kwambiri. Ayi... Masamba atadzazana, pansi. Ndipo ine ndinayamba kukwera kulowa mu nkhalangoyo.

¹¹⁴ Ndipo Chinachake chinati kwa ine, “Ndi agologolo angati amene iwe ukuwafuna mmawa uno?”

¹¹⁵ Ine ndinati, “Chabwino, ine ndakhala nawo handiredi ndi fortini chaka chino, kapena handiredi ndi seventini.” Ine ndinati, “Ngati ine nditakhala ndi atatu ena, iwo angapange handiredi ndi twente. Izo zingapange nambala yofanana kuti pakhale polokezera.” Ine ndinati, “Chinthu china chimene chingakhale, ndipatseni ine sikisi kuti nditengere kwathu.” Chimene, ine ndimawakonda iwo bwino kuposa nyama iliyonse imene ilipo yoti nkudya. Ndipo ine ndinati, “Ngati nditangopeza atatu ena.” Ine ndinayenda chokwera kudutsa mnkhalangomo patsogolo pang’ono. Ndipo, oh, panalibe aliyense. Asaki abwino, monga Charlie ndi iwo, anapeza mmodzi. Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine...”

¹¹⁶ Chinachake chinati, “Nena kwa iwo. Yankhula agologolo atatu ndipo iwe ukhala nawo iwo.”

¹¹⁷ Ine ndinati, “Zimenezo zinachitikapo kamodzi.” Chotero ine ndinaima pambali pa mtengo waung’onowo, mochedwa madzulo, kumbali ya mmphepete.

¹¹⁸ Ndipo Kudzoza kumeneko kunabwera mokula kwambiri mpaka ine ndimalephera ngakhale kuti ndiyimirire pa nthaka, ndipo anati, “Yankhula! Chimene utanene, usakaikire, ndipo iwe ukhoza kukhala nacho chimene iwe wanena.”

Ine ndinati, “Ine ndipeze agologolo atatu.”

Iye anati, “Kodi iwo achokere kuti?”

¹¹⁹ Ine ndinati, “Mmodzi abwere kuchokera mbali *iyi*, mmodzi achokere mbali *iyi*, ndipo winayo abwerere mbali *iyi*.” Kuzipanga izo mowonjeza. Mulungu samasamala momwe zikuwonekera mowonjeza. Iye ndi Mulungu wa zochitika.

¹²⁰ Ndipo pamene ine ndinaima pamenepo kwa pafupifupi maminiti pang’ono, ine sindimakhoza kumva kuwombera pozungulira, anyamata ena onsewo, kuzungulira paliponse. Ine ndinapezeka ndikuyang’ana mmbuyo mwanga, kutali uko mu nkhalango, pafupifupi mayadi nainte, ine ndinaganiza chinachake chinali pa chitsa. Ine ndinayang’ana icho. Patapita kanthawi iye analumphapo, ndipo iye anali gologolo wotuwa. Patali kwambiri, njira yonse kudutsa dzenje, ndi pamwamba pa chitunda. Pamene iye anabwera motsatira mbali ya mtengowo, ndinamuwombere iye. Ndipo iye anali pafupifupi mayadi nainte, ndipo iyo inapha iye. Ine ndinati, “Alipo mmodzi. Ine ndikhoza kungotembenuka ndi kuyang’ana mbali ina iyi, kwa enawo,

chifukwa iwo akubwera.” Mukuona? Mulungu amakhala nayo njira yobweretsera zinthu kwa iwe, kukupangitsa iwe kukhala wotsimikiza zomwe ukuziyankhulazo.

¹²¹ Kudzoza Kumeneko kunali kutachoka kwa ine pamenepo. Chabwino, ine ndinayembekezera ndipo ndinayang’ana mbali *iyi* kwa pafupifupi ora. Palibe chinachitika. Ine ndinali ndikuzizidwa. Ine ndinaganiza, “Ndithudi, ngati umenewo uli Mzimu Woyera umene ukundiiza ine zinthu zimenezo, izo zidzakhala ndendende basi. Chifukwa, pamene Kudzoza kunali pa ine, ine ndinayankhula mawu amenewo, ndipo izo zikuyenera kukhala mwanjira imeneyo.”

¹²² Tsopano mvetserani mwatcheru kwenikweni kwa izi. Ndipo izi zikhala zikujambulidwa pa tepi. Izo zidzapita konsekonse pa dziko lapansi.

¹²³ Tsopano ndiyeno, kumanzere kwanga, ine ndinapitirira kumayang’ana. Patapita kanthawi, ine ndinayang’ana mmwamba. Pa mtengo, ndikubwera mozungulira mtengo wa beech, apo panabwera gologolo wotuwa. Ine ndinati, “Ndendende basi mbali imeneyo. Uko nkulondola, Ambuye.” Ine ndinapotoloka, ndinadzuka kuti ndimuwombere iye, ndipo apo panabwera gologolo winanso. Ine ndinati, “Alipo awiri, chimodzimodzi basi. Pangani atatu anga.” Ndipo ine ndinadzuka, ndinawombera gologolo woyamba. Winayo anayenda kupita pansi pa chipikacho. Ine ndimakhoza kumuwona iye akudya—mtedza wa mu mtengo, kapena chinachake, pansi pa chipikacho. Chipikacho chinali pafupifupi chachikulu *chomwecho*, kumapeto kwake, chinadzuka pafupifupi phazi. Ine ndimakhoza kumuwona gologolo. Ine ndinamupha woyambayo.

¹²⁴ Ine ndinati, “Tsopano ine ndimupha winayo.” Ine ndinaititsira pansi, ndinayika tsitsi lopingasa limenelo pamwamba pa khutu lake, osadutsa mayadi forte, fifite kutali, ndipo ndinawombera ndi kumenya chipikacho. Ndipo gologoloyo sanatengeke nkomwe. Ine ndinaika chipolopolo china mmenemo. Ndipo iye anatembenuka, anapita pansi pa chipikacho, anapita kumathero enawo. Chabwino, ine ndinaikonzezeretsa ndipo ndinailunjikitsa mopambana mmene ndikanathera. Ndipo ine ndinali nditangophonya ka faivi kokha chaka chonse. Kenako ndinaititsira mmusi, kuwombera kwangwiro basi, ndipo ndinagwiranso chokhethemulira kachiwiri, ndipo ndinawombera pafupifupi mainchesi foro pamwamba pake.

¹²⁵ Ine ndinati, “Ine ndiyenera kuti sindinawombere molunjika.” Ndipo kenako ndinayang’ananso. Gologoloyo anathamangira mmwamba ndipo anapita ku mbali ya nkhalango, cham’mbali kuchokera kwa ine. “Chabwino,” ine ndinati, “Ine sindinawombere molunjika. Ine

ndingomuwombera iye cham'mbali ndiye, kumbali ya mchifuwa." Ndipo ine ndinadzuka ndipo ndinaika tsitsi lopingasalo. Ine ndinaganiza, "Mwinamwake ine ndazizidwa, ndipo ndikunjenjemera." Ine ndinaganiza, "Ine sindinali nditazizidwa ndi kumagwedezeke pamene ndimawombera winayo."

¹²⁶ Chotero ndiye, chimodzimodzi basi, pafupifupi miniti kapena awiri motalikana. Ndipo ine ndinagwira chitsamba, ndipo ndinachiyika icho mdzanja langa, ndipo ndinaigwira mfutiyo mothinita kwenikweni, ndipo ndinaiyika iyo pa chifuwa, pa chifuwa cha gologoloyo, ndipo ndinaikoka mfutiyo. Ndipo ndinawombera phazi pansi pake. Ndipo ine ndinakoka kuti nditenge chipolopolo china, ndipo mfutiyo inali yopanda kanthu. Pamene ndinali kuzilongedza, ine ndinati, "Ine ndimupeza iye ngati iye ati ayime pamenepo." Ndipo pamene ine ndinafika. . .

¹²⁷ Gologoloyo anapita mmwamba kudutsa mmitengoyo. Ine ndinayima pamenepo. Ine ndinaganiza, "Chiyani? Pali kuwombera kutatu, kolunjika, ndaphonya. Ndipo ine ndaphonyapo ka faivi mwa handiredi ndi fortini." Ine ndinati, "Izo zingatheke bwanji, kuti mfuti yanga iphonye?"

¹²⁸ Ndipo basi pomwepo izo zinabwera kwa ine. "Iwe sungakhoze kumuwombera gologolo uyo mwanjira imeneyo. Iye anali woti abwere kuchokera mbali imeneyo." Mawu a Mulungu ndi angwiro. Sindikanakhoza kumuwombera iye kuchokera kummwera. Iye amabwera kuchokera kumpoto.

¹²⁹ "Oh," ine ndinati, "Ine ndingotembenuka chozungulira mbali *iyi*, ndiye, ndi kumayang'ana kumpoto mpaka iye abwere." Ine ndinayika zipolopolo zambiri mu mfuti, ndipo ndimayang'ana. Chaching'ono. . . Ine ndinati, "Ngati iye abwere, iye ayenera kudzakhala pafupi kwambiri." Ine sindimakonda kumuwombera pafupi. Uwo si ukatswiri. Izo sizabwino kuchita zimenezo. Chotero mmodzi anali. . . kuwirirako kumeneko, ine ndinati, "Chabwino, ine ndiyenera kuti ndimutenge uyu amene akuchokera kumpoto, chifukwa ine ndinati mbali imeneyo." Chotero ine ndinaima mbali *iyi*, ndikumayang'ana.

¹³⁰ Ndipo ine—ine ndinati, "Ine ndikuganiza. . . ndachedwa." Ine ndinati, "Kotala isanakwane foro, tsopano foro koloko. Ine ndiyenera kuti ndichokepo, chifukwa, ndi awiri amenewo, chifukwa anyamatawo akundiyembekezera ine." Ndipo chotero ine ndinadikirira kanthawi pang'ono. Foro koloko inabwera, maminiti atatu itakwana foro.

¹³¹ Ine ndinati, "Chabwino, ine ndipita ndikatenge agologolo anga." Ine ndinapita mmwamba ndipo ndinakatenga agologolo, ndinabwerera, kuli mdima kwambiri ine sindimakhoza kuwona konse mu dzenje. Ine ndinayamba kutsika dzenjelo. Ndipo

pamene ine ndinali kupita pansi pa dzenjelo, kunali mdima, ndipo ndinadutsa pamene ine ndinali nditaima.

¹³² Chinachake chinati kwa ine, “Kodi iwe supita mmwamba umo ndi kukamutenga gologolo ameneyo?”

¹³³ Ine ndinati, “Ine ndimuwona bwanji iye tsopano?” Ndi kupenya kwakung’ono kwa telesikopu, kochepe kwambiri, kwakung’ono, kupenya kwa chandamale; panalibe kuwala kokwanira kuti ndiwone, mapazi pang’ono patsogolo panga. Ine ndinati, “Ine ndimuwona bwanji iye?”

¹³⁴ Anati, “Koma iwe unanena kuti pakhala winanso.” Oh, ine ndikukhumba ine ndikanangopanga zimenezo, mwanjiraina ine ndikanamupeza, mukuwona chomwe icho, eya, icho, chimene icho chimatanthauza kwenikweni, mzanga. Mukuona? Pansi pa Kudzoza kumeneko, sanali ine amene ndinanena zimenezo. Anali Mulungu amene ananena zimenezo. Ndipo ine ndinayenda masitepe angapo. Anati, “Tembenukani ndipo ubwerere cha kumpoto. Gologolo wako ali kumeneko.”

Ine ndinapita, ndinatembenuka. Ine ndinati, “Ambuye Mulungu, ine sindikaikira, mpang’ono pomwe.”

¹³⁵ Ine ndinayamba kuyenda kubwerera kumpoto. Pali amene akhala pano amene akuzidziwa izi. Ndinayamba kuyenda kubwerera kumpoto. Ndipo pamwamba pa chitunda, mayadi fifite kapena sikisite kutalikira kwake, gologolo anathamangira mumtengo, kuwala kokwanira basi kumene ine ndimakhoza kumuwona iye. Ine ndinafufuza ndi choyang’anira changa, zonse chokwera ndi chotsika mtengowo. Panalibe gologolo, ine ndikanakhoza kumupeza. Patapita kanthawi ine ndinaganiza kuti ine ndinawona mfundo pa mtengo, pamwamba apo, yakuda kwambiri. Ine ndinati, “Chabwino, ine ndiyesera chimenecho, mulimonse.” Ndipo ndinawombera. Ndipo pamene ine ndinatero, gologolo anathamangira mozungulira mtengowo ndipo anathamangira pansi. Ine ndinamumva iye akugunda nthaka. Ine ndinaganiza iye walumphapo.

¹³⁶ Nthawi yomweyo imene izo zinachitika, pafupifupi mapazi twente kuchokera pamenepo, wina anathamanga pa mgwalangwa woyera. Ine ndinati iye wamuthamangitsira pansi mmodziyo ndipo wakamuthawitsanso mzake winayo. “Tsopano, ndithudi, Ambuye, Inu simundilola ine kuti andisowekere ameneyo, ine nditatha kunena kale pansi pa Kudzoza kuti izi zichitika. Ndipo Inu mukutsimikizira utumiki wanga. Aka kakhala ka chisikisi kamene Inu mwatsimikizira izo kwa ine.” Nambala ya munthu, ka *sikisi*. Ine ndinati, “Inu simundilola ine andisowekere ameneyo.” Ine ndinayang’ana,ponse mmwamba ndi pansi pa mtengowo. Ndipo kumtunda uko, ine ndinaganiza kuti ndinawona masamba ena. Ine ndinawona chinachake chikuyenda mmenemo. Ine ndinakweza ndipo ndinawombera.

Ndipo gologoloyo anagwera pansi, pamwala wafa. Ndimapita ndikukwera phirilo, ndikusangalala ndi wokondwera.

¹³⁷ Ine ndinapita ku mtengo woyamba, kumanzere kwanga, ndipo apo panagona gologoloyo. “Chabwino,” ine ndinati, “Ine ndikudziwa ine ndamupeza mmodzi ameneyo, koma ine sindinali wotsimikiza za mmodzi uyu.” Ine ndinati, “Ndiye, Ambuye, Inu mundipatse ine mmodzi kuti pakhale muyezo wabwino.”

¹³⁸ Ine ndinapita kukamufufuza gologolo winayo, sanali kumeneko. Ndipo ndinayang’ana, ndipo ndinayang’ana, ndipo ndinafufuza pansi pa masamba ndipo ndinakweza zidutswa zazing’ono za chipika, ndi kung’amba chipika chakalecho. Ndipo apo panalibe koma chipika chimodzi chiri mkati mwa mayadi sarte, ndipo ine ndinaching’amba icho chonse mzidutswa. Ndinayang’ana pansi pa m’mbali, ndipo ndinagwira manja anga mmasamba, ndipo ndinamverera. Panalibe gologolo pamenepo, paliponsepo.

¹³⁹ Pamwambapo, panali chitsa chachikulu chakale pamwamba pa phirilo. Ine ndinapita pamwamba, chitsa chaching’ono chija. Apo panali kabowo kakang’ono kwambiri. Ine ndinamverera mmenemo, ndipo ine ndinaganiza kuti ine ndinamverera gologolo wanga, akukwera ndi kumatsika. Pamene ine ndinali... Ine ndinati, “Chabwino, ine sindingakhoze kufika kwa iye. Kotero, mmawa, ine ndiwabweretsa anyamatawo kuti abwerere ndi kudzamutenga iye. Ine ndiyenera kuti ndipite ndikawauze iwo.” Ndipo ine ndinapita uko kwa M’bale Charlie. Ndinatseka bowolo, ndinapita uko kwa M’bale Charlie ndi iwo, ndipo ndinakawauza iwo.

¹⁴⁰ Ife tinapita ku nyumba yawo usiku umenewo, ku mgonero. Ife tinali kusangalala mu Kukhalapo kwa Ambuye. Ndipo pamene, ndisanapite kokagona, M’bale Charlie uko anamufunsa M’bale Tony Zabel, kumbuyo uko, kuti atsogolere mu pemphero.

¹⁴¹ Tsopano, ine sindikunena izi kuti nditsutsane kapena kumuda M’bale Tony. Iye ndi mmodzi wa njonda ya Chikhristu yabwino kwambiri imene ine ndikuidziwa. Koma, kuti ndingokuwonetsani inu momwe Ambuye amagwirira ntchito. Tony, mu pemphero lake usiku umenewo, anati, “Ambuye Mulungu, mulole izi zidziwike kwa ife kuti m’bale wathu akutiuza ife choonadi, kuti mawa iye akamupeza gologolo ameneyo mu chitsa.” Ameneyo anali...

¹⁴² Ine sindinanene konse kuti ndikamupeza gologoloyo mu chitsa, pansi pa Kudzoza. Ine ndinati, “Ine ndinamuwombera gologoloyo.” Ndithudi, ine ndinalephera kuti ndimupeze gologoloyo, chifukwa, ngati ine ndikanatero, izo zikanapanga zochuluka kuposa zomwe ine ndinanenazo. Ndendende basi zimene ine ndinali nditanena, pansi pa Kudzoza kumeneko,

ndicho chimene Mulungu anapereka. Chotero, ine sindinanene kalikonse ka izo.

¹⁴³ Mwaona, ndi momwe, nthawi zambiri, anthu amati, “M’bale Branham ananena *zakuti-ndi-zakuti*.” Pamene M’bale Branham anena chirichonse, izo sizimakhala ndi kanthu kochita ndi zimenezo. Koma pamene Mulungu anena izo, izo zimakhala zoonza Mwamuyaya.

¹⁴⁴ Koma M’bale Tony sanazimvetse izo. Iye anati, “Ngati gologolo ameneyo ali pamenepo, ndiye ife tidzadziwa m’bale wathu watiuza ife choonadi.” M’bale Wood, M’bale Charlie, onse a iwo, anazitenga zimenezo. Ife sitinanene kanthu. Ine ndinagona ndi M’bale Tony usiku umenewo.

¹⁴⁵ Mmawa wotsatira, pa gome, ife tinali kuyankhula, za, “Oh, ilo linali tsiku lowopsya.”

¹⁴⁶ Ndipo M’bale Tony anati, “Chabwino, pali chinthu chimodzi, M’bale Branham akamtenga wake pa chitsa, mmawa uno, kuchokera mu mtengo.”

¹⁴⁷ Ine ndinati, “M’bale Tony, ine sindinanene kuti gologoloyo anali pamenepo. Ine ndinati ine ndimakhoza kumumverera iye, pamene iye amadzuka, iye amagwa.”

¹⁴⁸ Iye anati, “Iye adzakhala pamenepo. Iye adzakhala mu chitsa kumene.” Iye tinakwera mmwamba. Ndipo pamene ine ndinaisiya galimotoyo, ine ndinayamba kubwerera mmbuyo kachiwiri ndi kuti, “Pali chinachake cholakwika. Ine kulibwino ndimuuze Tony tsopano. Chifukwa, ngati gologolo ameneyo sali mu dzenje limenelo, mu chitsa chimenecho, ine ndibwerera wopanda gologolo nkomwe, ndiye molingana ndi momwe iye anapempherera usiku wathawu, iye azikhulupirirabe kuti ine ndinanena bodza.” Ine ndinati, “Mulungu, Inu mukudziwa, ndi Baibulo langa, kuti ine ndanena choonadi chowona.” Ndipo Mulungu akudziwa kuti icho ndi choonadi, ndinanena choonadi basi.

¹⁴⁹ Ndipo ine ndinapitirira. Chinachake chinangondiwongolera ine. Ndipo ine ndinapita ndikuyenda kudutsa mu nkhalango, ndikusaka. Ine ndimapitirira ndikuganiza, “Bwanji ngati gologolo ameneyo sali pamenepo?” Iye anandipatsa ine mpeni wake wosakira, kuti ine ndizikhoza kudula dzenje lokulirapolo, kuti ndizifikiramo ndi kumutenga iye.

¹⁵⁰ Ndipo Chinachake chinati kwa ine, “Ngati palibepo pamenepo, kapena ngati iye ali mmenemo, nchiyani chikupangitsa kusiyanitsako?”

¹⁵¹ Ine ndinati, “Iye adza...Iye sandikhulupirira ine. Iye anapemphera ndipo ananena, kuti, ‘Ngati ife timupeza gologoloyo, inu mudziwa kuti m’bale wathu watiuza ife choonadi.’”

¹⁵² Ndipo Kudzoza kwakukulu kuja kunabwera, anati, “Ingonena kuti gologoloyo akakhala ali pamwamba apo, ndipo iwe ukamupeza iye.”

¹⁵³ Ine ndinaganiza, “Ndithudi, Ambuye, ndithudi izi zikhala nthawi zisanu ndi ziwiri, molunjika, pamene Kudzoza uku kuli pa ine.” Ine ndinati, “Kodi ameneyo ndi Inu?”

Iye anati, “Nena chimene iwe ukufuna.”

Ine ndinati, “Ine ndikamupeza gologolo ameneyo.” Kudzozako kunandichokera ine.

¹⁵⁴ Ine ndinkasaka mpaka hafu pasiti naini, zomwe ife timayenera kuti tichite. Akubwera uko, ndipo amapita kukatenga agalu ena ndiye, iwo ankaganiza kuti iwo anali. Ndipo ine ndinapita pamwamba pa phiri pa hafu pasiti naini, ndinayang’ana mu dzenje, ndinamverera pozungulira, kudulidwa. Panalibe gologolo pamenepo, nkomwe, mu dzenjelo. Ine ndinamvereraponse pozungulira. Tsopano, chimene ine ndinali kutola chinali mizu yaing’ono yabwino ya udzu, kapena mizu ya mitengo imene ndinali ndikutola, ndi kumaimverera iyo ikugwa pa mtengowo, pamene ndimalowetsa mkati mtengowo, ndi kumaikokera iyo pamtunda monga *choncho*. Ine ndimaganiza ndinali kutola gologoloyo. Ndipo iye anali kusesereka kuchoka pa mtengowo, koma inali mizu yaing’ono ndi zinthu. Panalibe gologolo pamenepo. Ine ndinaganiza, “Tsopano kodi ine ndichite chiyani?”

¹⁵⁵ Ine ndikuti, “Ndi izi apa, hafu pasiti naini. Ine ndiyenera ndizibwerera.” Ine ndinatenga mfuti yanga ndipo ndinayamba kutsika phirilo.

¹⁵⁶ Ndipo Chinachake chinati, “Kodi iwe sunanene kuti iwe umupeza gologoloyo?”

Ine ndinati, “Kodi ndimupeza kuti iye?”

¹⁵⁷ Mulungu pokhala woweruza wanga wakachetechete, ndi Mawu Ake apa. Ndipo ndine bambo wa usinkhu wa zaka fifite, mlaliki wa Uthenga, ndaima pa guwa ili. Chinachake chinati, “Tayang’ana pansi pa chidutswa chaching’ono icho cha khungwa.”

¹⁵⁸ Ine ndinati, “Ambuye, ine sindingakukaikireni Inu popanda chifukwa.” Ine ndinayenda ndikupita kukatola khungwalo, ndipo pamenepo panalibe gologolo. Ine ndinaganiza ine. . .

Basi ine ndisanachite zimenezo, chinachake chinati, “Bwanji ngati iye sali pamenepo?”

¹⁵⁹ Ine ndinati, “Oh, iye akakhala pamenepo.” Ine ndinakatola ilo ndipo pamenepo panalibe gologoloyo. Ine ndinayang’ana pansi, ndi kudabwitsidwa. Ine ndinawona kachidutswa kakang’ono kwambiri kotuwa kakutulukira kuchokera pansi pa tsamba. Ine ndinakakokera iko mmwamba, ndipo apo panali

gologoloyo. Kuzipanga izo ndendende basi, chimene Iye ananena kuti achita.

¹⁶⁰ Ndinayamba kumatsika phirilo ndipo ndinakawauza iwo za izo, ndipo ife tinasangalala. Ndipo pamene ine ndinadzafika ku galimoto, Charlie, ataima apo pomwe, Banks, iwo anali akuyankhula, “Kodi izo sizinali zachirendo kuti Tony anganene chinthu ngati chimenecho mu pemphero lake, chimodzimodzi monga momwe iye amumakondera M’bale Branham? Ndipo iye angakaikire bwanji mawu ake ndi kunena zimenezo?” Mwaona, iye ankayenera basi kuti anene zimenezo mwanjira imeneyo, pakuti Mulungu anali akudziwa kuti ine ndikanadzaima pa guwa ili mmawa uno ndi kumadzanena chinthu chomwecho. Iwe umayenera kusamalitsa zimene munthu akunena, ndi zimene Mulungu akunena. Zimene Mulungu akunena ndi zoonza.

¹⁶¹ Ndiye ndinaganiza, “Chabwino, matamando akhale kwa Mulungu!” Ine ndinapita kumeneko. Ife tinali ndi nthawi yopambana. Tinabwera kunyumba.

¹⁶² M’bale George Wright, kwa zaka, wakhala akupanga vinyo wa mgonero. Ndiye ine ndikutseka. wakhala akupanga vinyo wa mgonero kwa mpingo. M’bale Roy Roberson kumbuyo uko, anandiyimbira ine ndipo anati, “M’bale Branham, tiyeni tipite uko ndipo tikatenge vinyo wa mgonero kuchokera kwa M’bale Wright,” yemwe wakhala apa, iye ndi banja lake.

Tsopano mvetserani kwa izi mwacheru, pamene ife tikutseka. O Mulungu!

¹⁶³ Ife tinapita kwa M’bale Wright, molawirira mmawa, ndipo, mwa chizolowezi, tinalandiridwa mwamphamvu. Ndipo ife timayankhula za vinyo. Ndipo kenako Edith wamng’ono, mtsikana wamng’ono wolumala atakhala pamenepo, yemwe ine ndimamukonda, monga ife timachitira kuno ku kachisi; osati ine ndekha, koma kachisi uyu, monga iye anali mlongo wathu yemwe. Banja la a Wright lakhala banja lakale kwambiri, limodzi la iwo, ndi a Slaughter kuno. Roy Slaughter ndi iwo, ndi a Wrights, kapena Akazi a Spencer, iwo anali mwa a pakale kwambiri omwe akhala ali mu kachisi. Ine ndikuganiza a Wrights akhala akubwera kuno kwa zaka twente-faivi kapena twente-sikisi.

¹⁶⁴ Ine ndamupempherera ndipo ndamupempherera, mtsikana wamng’ono ameneyo. Ine ndapemphera, kuti ndimuwone Mulungu akumuchiritisa iye. Ndipo ine ndawonapo zosautsa, ngakhale zazikulu kuposa za iyeyo, zikuchiritsidwa. Ndipo ine ndasala kudya, ndipo ndapemphera, ndipo ine ndakhala ndikuyembekezera, ndipo ine ndawafunafuna Ambuye, ndi misonzi, kufuna machiritso a mtsikana wamng’ono ameneyo. Kanthu kakang’ono kosauka kanasautsidwa pamene iye anali khanda chabe, mwina kufa ziwalo ali mwana, zomwe zinapinimbitsa manja ndi mapazi ake aang’ono. Iye anavutika

kwa zaka zambiri. Ndipo pamene ife tinapempherera nthawi yoyamba, chifukwa cha iye, iye anasiya kuvutika. Zimenezozakhala chaka...zaka twente-sikisi zapitazo. Pamene iye adwala m'mimba, kapena kupweteka kwa dzino, mwamsanga pamene tikapita kuti timupempherere iye, ndimadziwa kuti Ambuye asamalira zimenezoz. Koma kusautsika kumeneko...

¹⁶⁵ Ndipo ine ndamuwona iye akukhala muno mchipinda, pamene olumala ena amadzuka ndi kumanyamukapo, ndi zosautsa ndi zina zotero. Ndipo nkumadabwa, “Bwanji mtsikana wamng’ono ameneyo sakuyenda? Ambuye, wonekerani pa iye. Mulole Mngelo wa Kuwala amufungatire mwanayo, kuti ine ndikhoze kuyankhula, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE.’” Ngati izo zikanakhala kuti ndi ineyo, ine ndikanaziyankhula izo. Koma izo si za ine. Izo ndi za Iyeyo. Ndipo ndinkaziyang’anira izo.

¹⁶⁶ Ndipo ife tinali titabwerera, iye ankafuna kalulu. M’bale Wood ndi ine tinapita uko ndipo tinakapha akalulu awiri, tinawabweretsanso iwo kwa iye. Iye anali atakonza kale chakudya chamadzulo, Akazi a Wright ndi iwo.

Ndipo pa nthawi imeneyo...

¹⁶⁷ Mlongo Hattie Mosier, iye anali atataya mwamuna wake. Ine ndinawakwatitsa awiriwo, zaka zina zapitazo. Iwo ali ndi ana awiri abwino. Ndipo M’bale Watt anaphedwa. Mnyamata wake yemwe anamupeza iye pansi pa traki yake, ataphwanyidwa atafa. Ndipo mnyamata wamng’onoyo anali ndi kusweka, ndipo chinachake chinachitika kwa iye. M’bale Wood ndi ine tinapita kumusi uko usiku wina, ndipo tinakakhala mpaka usikuwo, kumene amayi ake ndi amalume anali akukhala ndi iye. Ndipo Ambuye anamulola iye kuti akhale bwino, ndipo iye ali pano mmawa uno. Amayi ake anali ndi chidwi ndi iye. Usinkhu wa mmadini umenewo, anangoyamba kumayenda ndi dziko, usinkhu wa zaka fifitini, kapena chinachake. M’bale wake wamng’ono akubwera pa usinkhu wa zaka thwelovu, sartini.

¹⁶⁸ Mlongo Hattie Wright, nonse a inu mukudziwa, ife timamutcha iye Wright, dzina lake ndi Mosier, koma iye wakhala munthu wokhulupirika, mkazi wamng’ono, wapanyumba, amakhala mzipinda ziwiri, kutali komwe uko mmapiri. Kunja uko amakhala ndi fosholo ndi khasu, kuyesetsa kumapala chisoso mu chimanga, kuti azisamalira banja lake laling’ono pamodzi. Iye anagwira ntchito mokhulupirika.

¹⁶⁹ Pamene ine ndinali nditakhala pa tebulo, ndikudya chakudya chamadzulo, ine ndinali ndikufotokoza chimene chikhulupiro chinali. Ine ndinati, “Ndipo chikhulupiro chimakhala chonchi. Ngati nditawona masomphenya a M’bale Shelby atakhala *wakuti-ndi-wakuti*, ndi mmodzi aliyense momwe anakhalira.” Ndipo Mlongo Hattie anali atakhala kumbuyo komwe uko, cha ku chipinda chinacho. Iye samakhala ndi zochuluka zoti anene. Samatero konse.

¹⁷⁰ Ndiyeno pamene ife tinali kuyankhula, ine ndinati, “Ngati Ambuye atandiwonetsa ine masomphenya kuti chinachake chinali choti chichitika, ndiye ine ndingat, ndikhoza kuchinena icho. Ndicho chimene chimakweza chikhulupiriro changa.” Ine ndinati, “Pamene Ambuye andisonyeza ine chimene chikuti chichitike, ndiye ine ndimakhala ndi chidaliro. Izo zikhala mwanjira imeneyo.”

¹⁷¹ Pamene Iye anandisonyeza ine, ine ndinati, “Ine ndingabwere pomwe pano, ngati mtsikana wamng’ono ameneyo, wosautsika atakhala pamenepo, ndipo Ambuye atandisonyeza ine kuti iye achiritsidwa. Ine ndingabwere pomwe pano ndi kudzaima mnjira, kumawona ngati chirichonse chinali ndendende basi momwe Iye ananenera. Ndipo kenako nkudzati, ‘PAKUTI ATERO AMBUYE. Edith, dzuka ndipo yenda.’” Ine ndinati, “Inu mungawone miyendo yaing’ono imeneyo ikufutukuka, manja aang’ono awo akufutukuka. Ndipo iye angakhoze kudzuka kuchokera pamenepo ndi kumayenda, kwa ulemelero wa Mulungu,” ine ndinati, “ngati izo zingabwere monga chomwecho.” Ine ndinali ndikuwauza iwo za chondichitikira ichi. Ndipo ine ndinati, “Kodi inu mukudziwa... ine ndikufuna kuti ndikufunsemi inu chinachake.” M’bale Banks Wood anali atakhala pafupi ndi ine, pa gome. Ndipo wotsatira, atakhala, pamenepo, Mlongo Hattie anali atakhala kumbuyo komwe. Ndipo anyamatawo anali atakhala apa, ndipo Akazi a Wright, ndi Bambo Wright. Ndipo Shelby atakhala kumbuyo kumanzere kwanga.

¹⁷² Tsopano mvetserani. Musati muphonye ichi; ndikukusonyezani inu kuchita kwayekha kwa Mulungu.

¹⁷³ Ndipo pamene ife tinali kuyankhula, ine ndinati, “Ine ndikufuna ndikufunsemi inu chinachake. Nchiyani chinaika agologolo aja pamenepo? Munalibe agologolo mu nkhalangomo. Ine ndinali nditasaka ndi kusaka. Ndipo ine—ine sindine msaki wabwino kwambiri, koma ine ndasaka kuyambira ndiri mnyamata wamng’ono. Ndipo ine ndinali nditasaka pafupifupi, ndipo—ndipo iwo anali pa malo opusisa kwambiri, ndipo mwanjira yopusisa kwambiri imene ndingakhazere kuzitchulira izo.” Ine ndinati, “Nchiyani chinawaika iwo pamenepo?”

¹⁷⁴ Ine ndinati, “Ine ndikudabwa ngati izo ziridi, kuti utumiki wanga ukukonzekera kuti utenge kusintha, kuti Mulungu wa Abrahamu akutitimikizira lonjezo Lake, monga Iye anachitira kwa Abrahamu pamene iye anali pamwamba pa phiri, ndipo iye ankasowa nsembe ya izo, mmalo mwa mwana wake. Yehova-yire anachita chozizwitsa, ndipo anakamuyika mwanawankhosayo, mailosi handiredi kutali. Iye anali ndi ulendo wa masiku atatu. Ndipo munthu wamba aliyense akhoza kuyenda mailosi twente-faivi pa tsiku. Kenako iye anakwezera maso ake mmwamba ndipo anawona phiri patali. Ndiyeno anapita ku phirilo, ndipo anakwera pamwamba pa phiri.

Pamene, nkhusa kumbuyo uko, nkhusa, nyama zakuthengo zikanakhoza kuyipha iyo. Ndipo, ndiye, pamwamba pa phiri kumene kunalibe madzi. Kodi nkhusa imeneyo inafika bwanji pamwamba pamenepo? Chinachitika ndi chiyani? Mulungu ankasowa nsembe, kuti akatsimikizire kwa Abrahamu kuti Iye anali Yehova-yire. Mulungu yemweyo wa chirengedwe anayankhula mwanawankhusa kuti akhalepo. Tsopano, awo sanali masomphenya. Iye anamupha mwanawankhusa, ndipo magazi anatuluka kuchokera mwa chinyama chimenecho. Iwo sanali masomphenya, iye anali mwanawankhusa.”

¹⁷⁵ Ine ndinati, “Mulungu yemweyo,” aleluya, “Yehova-yire ameneyo, Iye ndi mochuluka basi Yehova-yire lero monga Iye anali pa phiri ndi Abrahamu.” “Iye akhoza kuperekabe chinyama, kwa ulemerero Wake. Agologolo awa sanali masomphenya. Ine ndinawawombera iwo. Magazi anatuluka mwa iwo. Ine ndinawakonza iwo ndipo ndinawadya iwo. Iwo sanali masomphenya, iwo anali agologolo.” Ine ndinati, “Yehova-yire yemweyo, akuyesetsa kuti atengere lonjezo Lake kwa ine, mu zovuta zanga ndi mu kutsika kwa malingaliro, Iye akhoza kuyankhula chosowa changa kuti chikhalepo, mofanana ndi momwe Iye ananenera chosowa cha Abrahamu kuti chikhalepo.”

¹⁷⁶ Ine sindinanene mochuluka zimenezo, mpaka, Mlongo Hattie, wakhala apoyoy akulira tsopano, anali asananene mawu, ndipo iye anati, “Icho si china koma choonadi.”

¹⁷⁷ Iye ananena chinthu choyenera. Iye ananena chimodzimodzi monga Banks ananenera kumusi uko. Ine ndinamva liwu lake, pamene ilo linkasesa kuchokera mmakutu anga, monga uko mu nkhalango.

¹⁷⁸ Akazi a Wright, akhala kumbuyo uko ndi mtsikana wawo wamng’ono, anali kuyesera kuti atanthauzire zomwe Edith ananena. Ine sindimakhoza kuwamva Akazi a Wright.

¹⁷⁹ Ndipo Kudzoza kwapamwamba uko kunadzasesa pa ine, kunati, “Umuwuze Hattie kuti iye wapeza chisomo pamaso pa Mulungu.” Ndani akanaganizira? Anati, “Umuwuze iye kuti afunse chirichonse chimene akuchifuna. Akatero iwe uyankhule icho, mwa mphatso iyi, nkukhalapo. Chirichonse chimene iye angachipemphe, uchiyankhule icho mu kukhalapo.”

¹⁸⁰ Ine ndinayang’ana kwa Mlongo Hattie. Nthawi yoyamba imene icho chinayamba chachitidwapo pa munthu. Ine ndinati, “Mlongo Hattie, pemphani chimene inu mukufuna. Mulungu apereka icho kwa inu.”

¹⁸¹ Kodi inu mukuganiza chiyani za zimenezo? Kodi izo zikufika mwa inu? Nthawi ka seveni Iye anakhala akutsimikizira izo, pa chinyama. Seveni ndi nambala yamphumphu ya Mulungu. Apa inali nthawi yoyamba pa munthu. Ndipo, Iye, kodi Iye anasankha chiyani, munthu wina wopambana, mtumiki

wodziwika kwambiri? Mkazi wamasiye wamng'ono wosawuka amene samakhoza nkomwe kulemba dzina lake. Mulungu amadziwa chimene Iye akuchita.

Anati, "Pemphani chimene inu mukufuna."

Hattie ananena kwa ine, "M'bale Branham, kodi inu mukutanthauza chiyani?"

¹⁸² Ine ndinati, "Upemphe chirichonse chimene mtima wako ukukhumba, ndipo icho chiperekedwa pomwe pano, kuti udziwe kuti Ambuye Mulungu wa Kumwamba amayankha, ndipo Malemba Ake ndi owona."

¹⁸³ Nthawi yanga yoyamba ndi mphatso yatsopano; Kudzoza kwanga koyamba. Ine sindimakhoza konse kumumva iye. Ndipo iye anayang'ana pozungulira. Ife tinali tikuyankhula zokhudza mlongo wake wamng'ono, wolumala. Ine ndinati, "Oh, sindikukaikira," mu mtima mwanga, "mu maminiti pang'ono Edith akhala akulumpha ku ulemelero wa Mulungu."

¹⁸⁴ Hattie anayang'ana pozungulira, ponse pozungulira. Ndipo iye anati, "M'bale Bill, chokhumba changa chachikulu ndi cha chipulumutso cha anyamata anga awiri." Chiyani... Bwanji, pamenepo sipakanakhala chinthu chokulirapo. Iye akanakhoza kupempha madola teni sauzande, iye akanakhala nawo iwo. Nanga bwanji akanakhala miliyoneya winawake akanapemphenso miliyoni ina? Mulungu ankadziwa chimene iye akanati achipemphe.

¹⁸⁵ Mlongo Hattie, pafupifupi, mboni seveni kapena eyiti zitaima pamenepo. Anthu nonse inu amene munalipo pamene izo zinkachitika, kwezani mmwamba dzanja lanu. Aliyense mchipinda chino, analipo, izo zinkachitika; wani, thuu, firii, foro, faivi, sikisi, seveni. Seveni a iwo. Eyiti a iwo. Eyiti a iwo analipo pamene izo zinkachitika.

¹⁸⁶ Ine ndinati, "Upemphe chirichonse chimene ukufuna. Chifukwa, Mulungu wachipereka icho kwa ine, kuti ndikupatse iwe, chirichonse chimene ukufuna."

¹⁸⁷ Ananena kuti anyamata ake amayamba kusochera pa kunyanyuka kwa anyamata. Ndipo anati, "Chipulumutso cha anyamata anga awiri."

¹⁸⁸ Ine ndinati, "Mwa chifuniro cha Mulungu, mwa Mphamvu ya Mulungu, ine ndikukupatsa iwe, mu Dzina la Yesu Khristu, chokhumba chako." Ndipo anyamata ake awiri anagwedezeka pansu pa Mphamvu ya Mulungu. Ndipo nyumba yonseyo inanjenjemera. Banks anagwera mu mbale yake. Shelby anagwira. Ndipo Hattie anakuwa mpaka inu mukanakhoza kumumva iye kwa midadada iwiri. Ndipo anyamata awiri amenewo, ali ndi misonzi ikutsikira pansu mmasaya awo, analandira ndendende chimene iwo anapempha, pomwe apo. Oh!

¹⁸⁹ Nthawi yoyamba yomwe izo zinayamba zagwiritsidwapo ntchito pa munthu. “Pemphani chimene inu mukufuna, ndipo icho chidzapatsidwa kwa inu.” Anyamata ake, akhala pamenepo ndi iye, mmawa uno.

¹⁹⁰ Kodi iye akanapempha chiyani? Nanga bwanji ngati iye akanapempha machiritso a mlongo wake wamng’onooyo? Nanga bwanji ngati iye akanati apemphe zimenezo? Mtsikana wamng’onooyo akanachiritsidwa, koma anyamata ake awiriwo nkutayika. Bwanji ngati. . .

¹⁹¹ Mkazi wamasiye wosauka uyo, yemwe anali atangondiuza kumene ine kuti anayesera kupereka ku mpingo uno madola fifite pa chopereka, choti chithandizire kumanga tchalitchi chatsopanochi. Ndipo M’bale Roberson sakanalandira icho, ndipo anangomulola iye apereke twente za icho. Ndipo ine ndinati kwa inemwini, pamene iye anali kuyankhula, “Ine ndimubwezera iye twenteyo.”

¹⁹² Koma Mulungu ananena kwa ine, mu mtima mwanga, tsopano, osati mwa masomphenya, mu mtima mwanga, “Pamene Yesu anali ataima, akumuyang’ana mkazi wamasiye akuponyamo makobidi atatu, pamene munali madola masauzande ataikidwamo, kodi iwe ukanachita chiyani?”

¹⁹³ Ine ndinati, “Chabwino, ngati ine ndikanakhala nditaima apo, ndikanati, ‘Ife sitikuzisowa izo, mlongo. Ife tiri nazo ndalama zambiri.’” Koma Yesu sananene konse zimenezo. Iye anamulola iye kumapitirira ndi kuchita izo, chifukwa Iye ankadziwa zomwe zinali kumathero kwa msewuwo.

¹⁹⁴ Chotero ndithandizeni ine, Mulungu monga woweruza wanga wakachetechete, Mulungu ankadziwa kuti izo zinalipo kumathero a msewuwo kwa iye. Ndipo ndinayendetsa dzanja langa mthumba mwanga, kuti nditenge kachikwama ka mthumba, kuti ndimubwezere iye madola twente ake awo, ndipo ndinati, “Mlongo Hattie. . .”

Koma Iye anati, “Usachite zimenezo.”

¹⁹⁵ Ndiyeno maminiti pang’ono, pamene funso labweretsedwa lokhudza Yehova-yire, iye anati, “Izo si kanthu koma choonadi.” Ndipo izo zinabwera kuchokera mu mtima wa mkazi wamasiye wosauka, Mulungu ankadziwa kuti iye akanadzapempha chinthu chachikulu kwambiri chimene chikanachitidwa. Bola ngati Kumwamba kulipo, pamene nyenyezi zidzapita, pamene sipadzakhalapo konse mwezi, sipadzakhalapo konse dziko lapansi, kopandanso nyanja, anyamata amenewo adzakhala moyobe kupyola mu Muyaya ndi Yehova-yire Yemwe anapereka lonjezo lachisavundi. malonjezo Ake sangakhoze kulephera.

¹⁹⁶ Ine ndikuyembekezera kubwera kwa msonkhano uwu kumusi kuno mu San Jose. Oh, ngati iwo udzangosefukira! Tsopano pamene Kudzoza kugunda, “Pempha chimene ukuchifuna.” Ine ndiri nacho chitsimikizo changwiwo kuti

pamene Iko kukhudza, ndi chirichonse chimene Mulungu achiyika kuti chifunsidwe, icho chidzakhala ndendende basi mwanjira imeneyo. Izo ziyenera kutero, “Pakuti ngati inu munena kwa phiri ili.”

¹⁹⁷ Mwaona, si inuyo kuyankhula, Si inuyo, Ndi Mulungu. Ndi inuyo, chotero—wodzipereka kwambiri kwa Mulungu.

¹⁹⁸ Tsopano penyani aneneri akale, pamene ife tikutseka. Aneneri akale, pamene iwo amawona Kudza kwa Ambuye Yesu, iwo amakhala mu Mzimu kwambiri mpaka kuti iwo ankayankhula ngati kuti anali iwoeni. Tayang’anani pa Davide mu Masalmo, Salmo wa 22, akufuula, “Mulungu Wanga, Mulungu Wanga, nchifukwa chiyani Inu mwandisiya Ine?” Osati Davide; anali Khristu, zaka eyiti handiredi mtsogolo. “Mafupa anga onse akuyang’ana pa ine. Iwo akuwombera milomo yawo pa ine. Iwo akugwedeza mutu wawo.” Anati, “Iye anawapulumsa ena, koma Iyemwini Iye sangakhoze kudzipulumutsa.” Davide, akuyankhula ngati kuti anali iyemwini. Koma uwo unali Mzimu wa Mulungu mwa iye; Khristu, akuyankhula pamenepo.

¹⁹⁹ Oh, Mulungu alemekezedwe, akuyenda kulowa mu Mpingo Wake, mu chidzalo cha Mphamvu Yake, akuyenda pakati pa anthu Ake, akutambasula mapiko Ake aakulu a chifundo. Mulole Iye alemekezedwe!

²⁰⁰ Ine ndiribe nthawi ya ulaliki wanga. Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

²⁰¹ Kodi alipo mmodzi pano, mmawa uno, kapena ndi angati a iwo ali muno, amene akudziwa kuti inu simunakonzeka pa nthawi ino kuti mukakumane naye Mulungu? Kodi mungakweze manja anu, ndi kuti, “Mundipempherere ine, M’bale Branham”? Ife sitingakhoze kukubweretsani inu ku guwa, chifukwa maguwa adzadzidwa. Mulungu akudalitseni inu, m’bale; inu, mlongo; inu, m’bale; inu, ndi inu kumbuyo uko, nonse pozungulira; inu, dona wamng’ono; inu, m’bale wanga; kumbuyo komwe mmbuyo, kuzungulira paliponse. Mulungu akuwona manja anu.

²⁰² Ngati Iye angakhoze kubweretsa mwanawankhosa nkukhalapo pamene kunalibe mwanawankhosa, ngati Iye angakhoze kubweretsa nyama nkukhalapo, ngati Iye amakhudzidwa ndi mtengo waung’ono wa mkuyu ukukula kumbali ya phiri, kapena kansomba kakang’ono, kakufa kakugona mmadzi, ndi mochuluka bwanji momwe Iye amadziwira chokhumba chanu! Ndi chanu. . . Zedi, Iye amatero. Iye akudziwa kuti inu mukumusowa Iye. “Pemphani, ndipo inu mudzalandira. Pamene mupemphera, mukhulupirire kuti inu mulandira chimene inu mwachipemphacho.” Kodi umenewo unali Mzimu Woyera umene unakweza dzanja lanulo? Ngati iwo unali, ndiye Kudzoza kuli pa *inu*. Ndiye pempherani, ndipo

mumukhulupirire Mulungu, ndipo inu mukhala nazo zomwe inu mwanenazo.

²⁰³ Atate Akumwamba, pamene tsiku lino likukula kuyandikira ku tsiku la pakati, ndipo ine ndakhala motalikitsa pano mmawa uno, pa nkhani iyi ya chisomo Chanu Chaumulungu, molingana ndi Mawu Anu. Izo zinalembedwa mu Malemba, kuti Yesu Ambuye wathu anati, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita, nayenso azidzazichita.” Ndipo ife tikudziwa kuti ntchito zimenezo ndi zoonza. Inu mukhoza kuzindikira malingaliro a anthu. Inu munamuuza Petro yemwe iye anali, chimene dzina lake linali, chimene abambo ake anali. Inu munamuuza Filipo pamene iye anamubweretsa Nataniele, kapena anamuuza Nataniele, kani, kuti Inu munamuwona iye ali pansa pa mtengo iye asanabwere. Inu munamuuza mkazi, pa chitsime, ndi amuna angati amene iye anali nawo. Oh, palibe chimene chiri chobisika kwa Inu. Inu munkadziwa zinthu zonse. Ndipo izo zinali ntchito Zanu. Ndiye, ife tikukuwonani Inu mukuyankhula kwa mtengo wa mkuyu uja.

²⁰⁴ O Ambuye, ine ndikukhulupirira kuti ora likudza posachedwapa, limene mikate ndi nsomba zidzachulukitsidwe. Padzabwera chilemba cha chirombo, posachedwapa. Kudzabwera chitaganya cha mipingo. Ndipo iwo adzaika chikwangwani, mpingo wogwirizana, kuti, “Palibe munthu angakhoze kugula kapena kugulitsa.” Ndipo Mpingo Wanu, izo sizidzawasokoneza iwo, pakuti Mzimu Woyera Wanu udzawatsogolera iwo ndi kuwadyetsa iwo, monga Inu munachitira Israeli mu chipululu. Ndinu Mulungu. Musatilole ife tiziphonye zimenezo, Ambuye. Mutilole ife tikhalebe, mokhulupirika. Mutilole ife tikhalebe owona.

²⁰⁵ Tsopano ine sindikudziwa basi pamene izi ziti zidzachitike kachiwiri, Ambuye. Mwinamwake mmawa uno, kachiwiri. Mwinamwake izo zichitika kachiwiri mu kachisi lero. Ndikudalira kuti izo zitero, Ambuye. Ndikudalira kuti Inu muika chikhulupiriro mmitima ya anthu, ndi kudziwa kuti ine sindinawasocheretse kapena kunena chinthu chimodzi cholakwika. Ine ndanena izo basi momwe izo zinabwerera, mwa kupambana kwa zimene ndikuzidziwa mu mtima mwanga, Ambuye, kuwawona mawu anga ndi kuwayeza iwo. Podziwa kuti Inu mwatsimikizira izo kwa ine, monga ine ndanenena, ka seveni. Ndipo podziwa, mwamsanga zitachitika zimenezo, pa munthu woyamba yemwe ine ndinayamba ndayankhula naye, iye anapeza chokhumba cha mtima wake, mphindi imene iye anayankhula.

²⁰⁶ Tsopano, Ambuye, alipo ochuluka amene akukhumba muno mmawa uno. Inu muyenera kuti mumudzoze wantchito Wanu, Ambuye. Ngati Inu mutangotumiza Kudzoza! Ndiroleni ine ndikhale nako Iko, mmawa uno. Ngati aliyense angasowe, Inu mungoyankhula izo kwa ine, Ambuye, pamene iwo aziyankhula,

kapena paliponse, aliyense yemwe Inu mukumufuna. Ndipo mulole izo zifike pochitika.

²⁰⁷ Tsopano, ine ndidziwa kuti zimene zanenedwazo ndiye, izo sizikhala ine, izo zikhala Inu, Ambuye, mukuyankhula. Ine ndikudzipereka ndekha kwa Inu, ndipo ine ndisanachoke ku utumiki uwu, choyimira chakale, cha masomphenya, ndi zina zotero, pa guwa ili pamene ine ndinapereka moyo wanga mwatsopano, kuchokera kukulalikirira Uthenga kupita ku zizindikiro ndi zodabwitsa, Ine ndikudzipereka ndekha kachiwiri mmawa uno, kwa Inu, Ambuye, kwa utumiki. Nthawi yoyamba imene izi zanenedwa. Nthawi yoyamba, Ambuye, imene Iwo wawonetseredwa. Apa pakhala mboni.

²⁰⁸ O Ambuye Mulungu, ngati chiripo chirichonse chimene Inu mungakhoze kugwiritsira ntchito dzanja la ine lakale ili, ndine Wanu, Ambuye. Nditengeni ine, ndipo ndiwumbeni ine, ndipo mundipange ine, ndipo mundichitire chinachake, Ambuye, chimene chiti chidzakupatseni ulemu ndi kukulemekezani Inu. Ufalitseni Iwo pakati pa atumiki ena. Utumizeni Iwo ku ngodya foro za dziko. Maora akuchedwa. Yesu akubwera.

²⁰⁹ Adalitseni anthu Anu, pamodzi. Apulumutseni otayika. Aliyense amene anakweza manja awo apa, mmawa uno, apulumutseni iwo, Ambuye. Apateni iwo Mzimu Woyera. Mulole miyoyo yawo iperekedwe kwa Inu.

²¹⁰ Mpingo wawung'ono uwu, Ambuye, abusa, ndi m'busa aliyense pano, mlaliki aliyense, mphunzitsi, membala aliyense wa mpingo wina uliwonse, O Mulungu, monga thupi la anthu, ife tikudzipereka tokha kwa Inu. Titengeni ife ndipo tigwiritseni ife ntchito, Ambuye. Ndife Anu, ndipo tikuyembekezera kubwera kwa Inu tsiku lina, mu mtendere.

²¹¹ Tsopano ngati pangakhale wodwala aliyense kapena wosautsika, mulole iwo achiritsidwe, mmawa uno. Mulole chisomo Chanu ndi madalitso Amuyaya zikhale pa iwo, pamene tiziwapempherera iwo, pa kuika manja athu pa iwo ndi kupemphera. Mulole Mzimu Woyera ubwere ndi kudzagwira ntchito imene Iye anaiyika kuti ichitidwe. Perekani izi, Atate. Kudzera mwa Yesu Khristu, ife tikupempha mdalitso uwu. Amen.

²¹² Ine ndakuuzani inu choonadi choona. Basi monga momwe Mulungu waziululira izo, ndipo wazichitira izo, ine moona mtima ndakuuzani inu choonadi. Ndipo tsopano ine ndikufuna modzipereka kufunafuna ndi kukhumba mapemphero anu. Ine ndikuzindikira kuti mwamuna wa usinkhu wanga, wausinkhu wa zaka fifite. . .

²¹³ Mmawa wina, ine ndinanena kwa mkazanga, “Ndiri kale fifite, wokonedwa. Ngati ine ndingamuchitire chirichonse Ambuye, ine ndiyenera kuti ndifulumire.”

214 Iye anati, “Bill, Mulungu anamuphunzitsa Mose zaka eyite.” Ndipo anati, “Iye akhoza kukuphunzitsa iwe kwa zaka zina fifite, kuti apeze utumiki wa tsiku limodzi kuchokera kwa iwe. Iye ali nawe cholinga, chotero ingoima njii.” Ine ndinaganiza kuti imeneyo inali nzeru yochuluka, “Ima njii.”

215 Mulungu amasuntha dzanja lirilonse molingana ndi dongosolo Lake lalikulu. Ingokhala njii. Musamayese kupitirira...kumayesetsa kuti mukankhe. Inu mukhala mukupita patsogolo pa Iye, mukatero. Ndi zabwino kwambiri kumayesetsa kutsatira kuposa kumatsogolera, chifukwa Iyeyo ndi mtsogoleri.

216 Tsopano, kwa mpingo wanga waung’ono pano, nkghosa zanga zapang’ono zimene zakhala zokhulupirika kwambiri, ndipo zandipempherera ine, konsekonse mdziko. Ine ndikukhulupirira kuti pali kugwedezeke kwina kwa padziko lonse lapansi kumene kukubwera. Zinthu izi ine ndakuuzani inu ndi choonadi. Pa Tsiku la Chiweruzo, ine ndidzakumana nanu inu kutsidya ndi nkghani yomweyo, moona basi monga ine ndaima pano.

217 Tsopano, ine ndikutsimikiza inu nonse mukhoza kuwona chimene icho chiri. Ndi kubwera kwa Kudzoza kopambana, kwakuya kwa Mzimu Woyera. Momwe ungafikire mwa Iko, ine sindikudziwa. Chinthu chokhacho chimene ine ndikuchidziwa, zimatengera Mulungu kuti akuyike iwe mwa Iko. Kotero, iwe uzingokhala mokoma, ndi modzichepetsa, ndi pafupi kwa Mulungu momwe iwe ungathere. Osamukaikira Iye. Kungokhulupirira kuti chirichonse chikugwira ntchito kwa ubwino basi, kwa iwe, ndipo chirichonse chigwira ntchito pozungulira mwabwino bwino. Mukuona?

218 Ingokumbukirani, ndinu nkghosa. Iye ndi Nkhunda. Ndipo nkghunda imatsogolera mwanawankghosa. Pamene...Ndipo mwanawankghosa ndi nkghunda zimakhala ndi chikhalidwe chofanana. Nkhunda ndi yofatsa kwambiri mwa mbalame zonse za mu mlengalenga. Mwanawankghosa ndi wofatsa kwambiri mwa zinyama zonse zapadziko lapansi. Kotero, mukuona, mizimu yawo ikhoza kugwirizana wina ndi mzake. Tsopano, nkghunda siyingakhoke kubwera pa nkghandwe. Mukuona? Iyo siyingakhale pamenepo. Nkghandwe ndi yakupha. Mwanawankghosa ndi wodekha.

219 Chotero, inu mukuona, ndi Mwanawankghosa ndi Nkhunda, ndipo wina akutsogolera mzake. Ndipo kodi mukuona kumene Nkhunda inatsogolera Mwanawankghosa? Njira yonse mpaka ku Gologota, kuti ikapachikidwe. “Ndipo Iye sanatsegule ayi kamwa Yake.” Pamene iwo anamulavulira Iye, Iye sanawalavulire konse mobwezera. Pamene iwo anamumenya Iye, Iye sanawamenye mobwezera. Iye anangomapitirira, akudziwa kuti Iye anali, kwa ulemelero wa Mulungu, Iye anali kuchita chifuniro cha Mulungu.

220 Mlongo Hattie, ife tiri pafupifupi usinkhu wofanana. M'bale George Wright apo, abambo ake, ndi anyamata ake, amayi, Shelby.

221 Ine ndikufuna ndinene ichi. Ine ndikuganiza inu mukudabwa chifukwa chimene ine ndinadzuka ndi kutuluka mnyumba mwamsanga monga ine ndinachitira. Ine sindinayambepo...Ine ndakhalapo kumene achikunja sarte sauzande anapulumutsidwa pa nthawi ina, South Africa, anabwera kwa Khristu. Ine ndikuganiza kuti kumeneko kunali Kudzoza kwakukulu kumene ine ndinayamba ndakumvererapo. Iko sikungafanizidwe nkomwe, mwanjira iliyonse, ndi kujaku kumusi uko kwa a George Wright, tsiku lina. Ine sindinayambe ndamvererapo chirichonse chonga Icho. Chipinda chonse chimangowoneka kuti chiri chabe—Kuwala kwa Ulemelero wa Mulungu.

222 Tsopano, Mlongo Hattie ali chete kwambiri ndi mkazi wamng'ono wauzimu, samakweza konse liwu lake pa chirichonse. Koma inu mukanakhoza kumva kufuula kwake, mdadadada wa mu mzinda, pamene Mzimu Woyera unakantha nyumbayo. Aliyense, aliyense pamenepo, anamverera Iwo. Izo zinali zodabwitsa. Ife tikhoza kukhala nthawi yaitali, koma, Mlongo Hattie, bola ngati pali kukumbukira mmalingaliro athu, ife tidzakhala tikukumbukira zimenezo, ndi Mlongo Wright.

223 Tsopano, kuti anthu akhoze kudziwa kuti ine ndinanena izo ndendende basi moona, kodi inu mungakweze mmwamba dzanja lanu, Mlongo Hattie, chotero, kuti, Mlongo Wright ndi inu nonse munali kumeneko, munali kumeneko basi, basi kuti inu mukhoze kuwona. Mukuona? Ndi amenewo apo.

224 Apa, imirirani, Mlongo Hattie. Ndi ameneyo mkazi wamasiye wamng'ono yemwe chozizwitsa chinachitikirapo, koyamba. Kulambalala anthu onse a mdziko, chinthu chimenecho kuchitikira koyamba kwa mkazi wosauka, wamng'ono, wodzichepesa wamasiye pamwamba pa phiri, pamwamba apo yemwe amayesera kulima mbewu ya chimanga kuchokera mu nthaka ya maenje kumeneko, kuti awasamalire ana ake. Ndi amene Mulungu anawalemekeza, nthawi yoyamba chiyambireni masiku a...a Yesu Khristu, ndipo anati, "Pemphani chimene inu mukuchifuna."

225 Ine ndinati, "Ine ndikumubetchera aliyense, mu Dzina la Ambuye. Pamene Mzimu umenewo ukhudza ndi kunena zimenezo, ine sindisamala zimene inu mukuzipempha, izo ziperekedwa."

226 Inu mukudziwa chifukwa chimene apamwamba sanamvetse izo, kapena anthu aakulukulu monga choncho? Ndi chifukwa chakuti Mulungu ankadziwa kuti iwo akanati adzafunse zinthu zomwe sizinali zabwino kwa iwo.

227 Iye amapereka Iwo kwa anthu amene Iye amadziwa kuti afunsa chinthu cholondola. Ndipo mkazi ameneyo akanatani... Chinanso chiyani? Ingondiuza ine chirichonse chimene iye akanafunsa chachikulu kuposa chimenecho. Amayi ake ndi abambo anapulumutsidwa. Mlongo wake wamng'ono anapulumutsidwa. Banja lonse linapulumutsidwa, kupatula anyamata awiriwo, pa nthawi imeneyo. Iwo anali asanapulumutsidwe.

228 Iwo ndi anthu osauka. Shelby anandiuza ine zopindula zake zowirikiza, za mbewu zabwino, iye amapeza madola sikisi handiredi pa chaka. Kumagwira ntchito mpaka mnyamatayo ali pafupifupi usinkhu wanga, ndipo ndi wosweka yense, chirichonse. Ndipo akugwirabe ntchito, kuwasamalira abambo ake ndi amayi, ndipo iwo ndi okalamba, ndipo akuyesetsa kumusamalira mlongo wake wamng'ono, wosautsika. Koma iye ndi wopulumutsidwa. M'bale Wright, onse a iwo, anapulumutsidwa.

229 Koma awiriwo anali asanapulumutsidwe. Ndipo Hattie anafunsa chipulumutso cha ana ake, malingana ngati kuli Umuyaya. Iye akanakhoza kupempha madola teni sauzande, ndi kuwapeza iwo. Iye akanafunsa chirichonse chomwe iye akanafuna. Koma Mulungu amadziwa chimene inu muti mudzapemphe, Iye asanaikse konse Kudzozako. Uko nkulondola.

230 Mlongo Hattie, ndi kulondola uko, kuti ine ndinanena kuti, "Pemphani chirichonse chimene inu mukuchifuna. Chirichonse chimene mtima wanu ukukhumba, mupemphe icho, Hattie"? Nkulondola uko, Mlongo Hattie? Mukuona? Mukuona? "Pemphani chirichonse chimene inu mukufuna kutero, izo ziribe kusiyana chomwe icho chiri. Pemphani icho. Mulungu ananena kwa ine, 'Ingoyankhula chimene iye wapemphacho, ndipo iye alandira icho.'" Ine ndinati, "Pemphani icho tsopano, basi chirichonse chimene inu mukuchifuna." Ndipo iye anachita icho.

231 Oh, m'bale, mlongo, kodi inu mukuzindikira tsiku limene ife tikukhalamo? Nthawi yaulemelo kwambiri, pamene Mulungu wa Kumwamba adzayike pakati pa anthu, kuti, "Pemphani chirichonse chimene inu mukuchifuna, ndipo Iye adzapereka icho kwa inu." Huh! Ndicho—icho ndi chakuya kwambiri kwa malingaliro anga. Ine ndikudziwa zimenezo. Koma ndikuyembekeza, mu mtima mwanga, ndikhoza kugwira zochulukira za Iko monga ine ndingathere. Iko, ziri basi... Ine ndakhala moyo pa Kumeneko. Ine ndakhala moyo pa Iko. Ine ndikupita chakumadzulo pa Iko. Ine ndimalowa mmisonkhano pa Iko. Ine ndikukhala moyo pa Iko. Mawu a Mulungu ndi olondola.

232 Tsopano, monga momwe ine ndikudziwira, ndicho chinthu chotsiriza choti chichitike. Ine sindikudziwa china chirichonse,

chomwe icho chingakhale, kungopereka kwa anthu, “Pemphani chirichonse chimene inu mukufuna, ziribe kanthu chimene icho chiri. Mungochipempha icho, ndipo icho chidzaperekedwa kwa inu.”

²³³ Ndipo kodi inu mukukhoza kuwona nzeruzo? Ndi angati akukhulupirira zimenezo, kuti mkazi ameneyo anafunsa chinthu chopambana chimene chikanakhoza kufunsidwa? Tiyezi tiwone inu. Kodi inu mungalingalire? A—mkazi ali ndi mlongo wosautsika, akanakhoza kupempha machiritso ake. Mkazi amene ali wosawuka, ndipo amayi ake ndi abambo, osauka, ndi onse a iwo osauka, akanakhoza kupempha ndalama ndipo nkuzipeza izo. Iye akanakhoza kufunsa kuti zaka ziwonjezeredwe ku moyo wake, ndipo akanakhala nazo izo. Koma iye anafunsa chinthu chachikulu chimene chikanakhoza kufunsidwa, chipulumutso cha banja lake losapulumsidwa, ndipo anachipeza icho. Amen. Ndicho chinthu chofunikiracho. Anachipeza icho, kuchokera kwa Mulungu yemweyo amene anapereka lonjezo. Iye ndi Mulungu. Oh, momwe ine ndikumukondera Iye!

²³⁴ Tsopano ife tikuti...Kodi alipo odwala aliwonse pano oti apemphereredwe? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Mkazi anayimba mausiku angapo apitawo. Alipo atatu a iwo, ine ndikukhulupirira, kuchokera ku California kapena chinachake, iwo anandiuza ine. Amene anati, “Ife tabwera kawiri kapena katatu, ndipo inu munapereka makadi a pemphero, ndipo manambala athu sanaitanidwe.” Ine ndinamupangira iye lonjezo, ngati iye angakhalebe, kuti ine ndingopempherera odwala mmawa uno.

²³⁵ Ndi angati anakhalapo muno pamene ife timakhala nako kuzindikira za mumtima ndi zinthu? Oh, nonse a inu, ine ndikuganiza, aliyense pano. Mukuona? Ife tikudziwa kuti izo nzoona. Ife tikusuntha kudutsa zimenezo tsopano. Oh, matamando akhale kwa Mulungu! Ife tikusuntha kudutsa zimenezo tsopano. Mwinamwake zimenezo zifika pochitika... Ine sindikudziwa chimene Mulungu ati achite mmawa uno.

²³⁶ Koma anthu inu amene mukudwala ndi osautsika, ine ndikufunsani inu kuti muzibwera, apang’ono pa nthawi. Mulole awa ku mbali *iyi* apa, abwere, kuti ife tikhoze kuwapempherera awa ku mbali *iyi* choyamba. Mwinamwake ine ndikhoza kuzigwira izo monga choncho. Bwerani komwe kuno, mlongo. Mudzangofola pomwe apa. Chifukwa ife tiribe...Iwo ayenera kuwatumiza iwo kumbuyo uko nkanjira komweko, pa chifukwa chakuti iwo abwerere pa malo omwewo.

²³⁷ Ine ndikhoza kudziwa momwe munthu wamng’ono uyu amayankhulira, mmawa uno, iye amakhulupirira mu machiritso Auzimu, ine ndikudziwa, ndipo amakhulupirira mu Mphamvu ya Mulungu. Kodi alipo mtumiki wina pano, mmawa uno, amene

ali—mtumiki amene amakhulupirira kuti Mulungu amachiritsa odwala? Ngati alipo, muloleni iye abwere kuno, mmodzi aliyense. Inu nonse mubwere kuno ndi kudzaima ndi ife pamene ife tikuwapempherera awa, odwala awa ndi osautsika, aliyense wa inu abale amene mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza odwala. Mulungu akudalitseni inu, bwana, bwerani kutsogolo, ife tikufuna kuti inu mubwere kuno ndi ife.

²³⁸ Tsopano ife sitikudziwa chimene Mzimu Woyera ungachite. Mzimu Woyera ukhoza, pa nthawi ino, kuchita monga momwe Iye anachitira uko kwa Mlongo Wright tsiku lina lija. Ine ndikudalira kuti Iye atero. Ine sindikudziwa. Inu mukumvetsa? Ndi angati akudziwa...? Chabwino, palibe ambiri a inu amene munachoka kuno, pamene masomphenya ankayamba koyamba. Ine sindikudziwa kuti ndi nthawi yanji yomwe iwo ati adzabwere, zomwe iwo ati adzachite. Chirichonse chiri mu chifuniro cha Mulungu ndipo chiyenera kulamuliridwa ndi Mulungu. Ndi angati akudziwa zimenezo? Mulungu sangakhoze kuwapatsa anthu zinthu zoti azizilamulira, iwoeni. Ngati iwo angatero, ndiye, inu mukuona, izo sizingakhale ali Mulungu. Izo sizingakhale Mulungu. Izo zingakhale... Ine ndikufuna kuti inu muganize apa, abwenzi, mu malo otsika aang'ono awa, koma momwe Ambuye mwamtheradi, M'bale Mike, kudutsa mthunzi uliwonse wa kukaikira, watidalitsa ife, ndipo anachita ndi kuchita chimodzimodzi basi zomwe Iye analonjeza kuti Iye akanadzachita.

²³⁹ Ndi angati anayamba amvapo za malingaliro apamwamba? Ambiri a inu mwatero. Ndizo—si kanthu basi koma nthano, zamizimu. Koma, inu mukudziwa, izo sizingakhoze... Zinthu zimenezo si zokhalitsa. Izo sizimakhala mopitirira. Iwo sangakhoze konse kupeza chogwirika chirichonse. Iwo amakhoza kukhala pamenepo ndi kukhala... Iwo amati, “Pali mzimu. Pali mzimu.” Ndipo iwo amayesetsa kuti atenge chithunzi cha izo, kapena chinachake. Iwo sangakhoze kuchita zimenezo. Mukuona? Kungoti palibepo pamenepo. Ndi zamaganizo, zopeka. Mukuona?

Koma chimene Mulungu amachita chimakhala changwiwo.

²⁴⁰ Pamene Mose anaponyera pansi ndodo yake, wamatsenga anaponyera pansi ndodo yake, nayenso. Izo zonse zinasanduka njoka. Nkulondola uko? Koma chinachitika ndi chiyani ndi ndodo ya Ayane ndi Ayambre? Ndodo ya Mose inameza izo. Ndipo pamene Mose ananyamula ndodo yake, iyo inali ili ndodobe. Koma ndodo yawo inali kuti? Mkati mwa ndodo ya Mose. Mukuona? Inu simukanakhoza kuyiwona iyo. Pamene Mulungu achita chirichonse, Iye amachipanga icho kukhala chenicheni.

²⁴¹ Tsopano iwo amandiuza ine, “Mzimu Woyera, inu mukudziwa,” iwo amati, “ndi anthu basi amene angozipukusa.

Ndi zammaganizo. Masomphenya amenewo ndi zinthu, izo ndi kuwerenga maganizo basi.”

²⁴² Chabwino, pamene George J. Lacy anafufuza chithunzi chija uko, pamene Mngelo uja wa Ambuye, ambiri a inu mwaima pano munachiwona Icho pa mtsinje, ndi nthawi zambiri, iye anati, “M’bale Branham, diso la makina la kamera iyi silimatenga kuwerenga maganizo.” Anati, “Kuwala kunali pamenepo. Ndi Zimenezotu.” Ndi zosatha. Ndi zoona. Chotero, inu mukuona, ndi Mngelo yemweyo wa Mulungu. Tsopano penyani Icho. Chikhalidwe cha Iye chimatsimikizira Chimenecho.

²⁴³ Pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iwo unkakhala mwa Ambuye Yesu Khristu, Yemwe anali Mulungu atawonetseredwa. Ndipo tsopano Yesu anati, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silindiwonanso Ine, komabe, inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezero a dziko lapansi. Ndipo zinthu zimene inu mukuchita, zimene Ine ndikuzichita, inunso mudzazichita.”

²⁴⁴ Tsopano penyani Iwo, pamene Iwo ubwera. Munthu akhoza kunena chirichonse, koma pamene Mulungu ayikira izo kumbuyo, izo zimapangitsa izo kukhala zowona. Tsopano penyani chikhalidwe cha Mngelo ameneyo. Pamene Iye amutengera munthuyo podzipereka kwambiri kwa Iye, Iye amachita chinthu chomwecho chimene Yesu ankachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi. Chifukwa, ife timakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu, ngati ife tibadwa mwa Mzimu Wake. Mukuona? Ndipo si chinthu cha nthanonso. Iwo umakhala ndi umboni wotsimikizira izo. Iwo umasonyeza kuti izo nzoona. Chotero chipulumutso chathu chimakhala mwamtheradi changwiro.

²⁴⁵ Mulungu wa Kumwamba, Amene anali nawo aneneri onse kuti aziyankhula za Kudza kwa Ambuye Yesu, ndipo Yesu, pamene Iye anabwera, Iye anakwaniritsa uneneri uliwonse, ambiri a iwo anakwaniritsidwa pa mtanda, “anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu,” ndi zimene Davide ananena, “Mulungu wanga, Inu mwandisiyiranji Ine?” Koma pamene Mulungu atumiza mneneri, mneneri akayankhula, Mulungu amazipanga izo kukhala zoona, ngati ali Mulungu. Ndi pamene Iye anati, kuti tiziwadziwa iwo. “Ngati iwo ayankhula, ndi zomwe iwo ananenazo zifika pochitika, ndiye muwakhulupirire iwo, pakuti ine ndiri nawo iwo; ngati izo sizitero, ndiye iwo ali—iwo siali. Iwo ndi aneneri abodza.” Iye anati, “Koma, tiziziyang’ana izo, kuziwona ngati izo zifike podzachitika.”

²⁴⁶ Tsopano taonani. Ngati... Mulungu, Amene ankayankhula mwa mneneri woyera, anayankhula za kudza kwa Mesiya, kwa ulemero ndi ulemu wa Mulungu.

²⁴⁷ Ngati ine nditadziwa yemwe ati adzakhale purezidenti mukugwa kwa masamba kotsatira, ndipo nkunena izo, umenewo

ungakhale uneneri. Uko nkulondola. Koma Mulungu samalosea monga chomwecho, basi kuti, oh, kungoti azisewera. Mulungu amachita chinachake kuti amulemekeze Iye. Mukuona?

Koma pamene Mesiya abwera, ndipo pamene Mesiya anachoka. . .

²⁴⁸ Ine ndikufuna kuti ndikufunseni, nonse inu Amethodisti, Abaptisti, Apresbateria, Akatolika, Achilutera, Achipentekoste, Nazarene, Pilgrim Holiness, nonse a inu, ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu chinachake. Kodi inu simukuganiza kuti Mfumu ya aneneri ija, Yesu, akanadziwa momwe angaukhazikitsire Mpingo Wake Womwe? Ngati aneneri onse ankayankhula za Iye, ndi kulozera kwa Iye, kodi Iye anawukhazikitsa Mpingo wa mtundu wanj? Pamene Iye ankachoka, Iye anati. . . Pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anamuza Petro, “Pa vumbulutso la Mawu a Mulungu,” Iye anati, “pa thanthwe ili Ine ndidzamangapo Mpingo Wanga, ndipo zipata za gehena sizidzakhoza kuwulaka Iwo.” Kodi si kulondola kumeneko? Chabwino. Pamene Iye anali. . .

²⁴⁹ Iye asanachoke, mu Marko 16, Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira.” Kodi Iye ananena zimenezo? “Mu Dzina Langa iwo adzatulutsa ziwanda, adzayankhula ndi malirime atsopano, adzagwira njoka, kumwa zinthu zakupha.” Iye ananenanso kuti, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.” Nkulondola uko? Ndizo zizindikiro zimene ziri zoti zizitsatira Mpingo Wake. Si chipembedzo. Ndi bungwe lokhazikitsidwa lodzozedwa ndi Mulungu, lodzazidwa ndi Mzimu Woyera, Mpingo wobadwira Kumwamba umene umachokera ku zipembedzo zonse, gulu lenileni lokhulupirira la anthu.

²⁵⁰ Atumiki awa aima pano angokhala nane. Ndife amuna. Iye ndi Mulungu, koma ife tiri pano kuti tizimuimirira Iye. Ife tiri pano kuti tizikuuzani inu kuti ife. . . Mulungu watitumiza ife kuti tidzachite ntchito iyi, kuti tidzaika manja pa odwala. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo.” Zizindikiro zimenezo, zizindikiro zonse zimene Iye anaziyankhula, zidzamutsatira wokhulupirira. Apa iwo ali, akutsatira. Iwo akutsatira.

²⁵¹ Ndipo Mulungu samalemekeza munthu. Chimene Iye anachita kwa Hattie, Iye akuchitirani inu. Chimene Iye anachita kwa akhungu, Iye akuchitirani inu, wakhungu. Chimene Iye amachitira ogontha, Iye akuchitirani inu. Chirichonse chimene Iye wachitira kwa wina aliyense, Iye akuchitirani inu, ngati inu mungokhulupirira. Nkulondola uko?

Tsopano, M'bale Teddy, ine ndikufuna kuti inu muziyimba *Kungo Khulupirira*.

²⁵² Ndipo pamene anthu awa akudutsa mu mzere, ndiye ife titenga mbali inayo. Ife tizidutsamo, tonse a ife tikuika manja pa inu, tikukupemphererani inu, kuti matenda anu achiritsidwe.

Ndipo izo zikhoza. Izo zichitika. Ndipo ine sindikudziwa chimene Mulungu ati adzachite. Ine ndangoima pano pakali pano, wosadziwa choti ndichite. Ine ndingopempherera odwala monga ine ndinamulonjeza winawake kuti ine ndidzatero. Kungowapempherera...

²⁵³ Lamlungu lapitali, kumbukirani, ine ndinakuuzani inu. Lamlungu lapitali anali—anali mavumbulutso, ndi zina zotero. Lamlungu lino ine ndipempherera odwala.

Tiyeni tipemphere tsopano.

²⁵⁴ Ambuye, ife tayima pano ngati antchito Anu. Ife tayima pamaso pa anthu Anu. Ife tiri pano. Ife sitikudziwa chimene Inu muti muchite. Inu mukhoza kuyankhula ndi lirime. Inu mukhoza kutanthauzira. Inu mukhoza kupereka masomphenya. Inu mukhoza kundipangitsa ine kuti nditenge dzanja la winawake, kwa vumbulutso. Inu mukhoza kuyankhula ndi kupereka ulamuliro, kuti, “Nena chirichonse chimene iwe ukufuna.” Ine sindikudziwa chimene Inu muti muchite, Ambuye. Ndipo mwinamwake Inu mukufuna kuti ife tiyike manja pa odwala. Ife sitikudziwa chimene icho chiri. Ife tikungofuna kukusangalatsani Inu, Ambuye. Ife taima pano, ngati antchito Anu. Ndipo awa ndi anthu Anu, ndipo ife tikuyesetsa kuti tiwathandize iwo, molingana ndi zomwe Mawu Anu akunena kuti tizichita. Ife tikuyesetsa kutsatira malangizo Anu. Ndipo ine ndikukupemphani Inu, Ambuye, kuti Inu mupereke kwa ife zimene ife tikuzisowa, kuti titumikire kwa anthu, kudzera mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁵⁵ Ine ndikufuna nonse a inu muweramitse mutu wanu pansu ndipo mupemphere. Pamene M’bale Wood, ngati inu mungathe...

²⁵⁶ Ndipo, abale otumikira, ine ndikukhulupirira ife tikanayima pomwe pano. Ndi angati ali muno? Foro a inu pano? Chabwino. Awiri ku mbali iliyonse uko, ndipo ine ndiyima patsogolo pomwe pa mzere, pomwe apa. Mukuona? Mphindi imodzi yokha. Tsopano, kuzungulira pomwepo, bwerani kuno, m’bale, wokondedwa. Tsopano, ndi zimenezotu, imani pamenepo tsopano, ndipo pamene iwo akudutsa. Osonkhana onse... Tsopano, ngati anyamata aang’ono inu mungasunthire mmbuyo pang’ono, kuti iwo azikhoza kumayenda nawo.

²⁵⁷ Tsopano, pamene ife tonse tikupemphera, muzipita molunjika ku yanu—mipando yanu pamenepo. Mu maminiti pang’ono, ine ndiyitanira mbali inayo.

²⁵⁸ Tsopano, mmodzi aliyense wa inu, osati atumiki okha, koma, nonse a inu muyenera muziwapempherera anthu awa. Inu simukudziwa chimene Mulungu angakuchitireni inu pamene inu mukumupempherera winawake. Nanga bwanji ngati inu mutati munene chinthu cholondola? Bwanji ngati... Apa pali mkazi wayima apa, amene akudwala kwambiri iwo ayenera kuti

amugwire iye. Nanga bwanji ngati pemphero lanu lingakhale chinthu cholondola, basi monga Banks ananena chinthu cholondola, monga Hattie ananena chinthu cholondola? Bwanji ngati inu mukhoza kunena chinthu cholondola, pemphero lanu, chomupangitsa Mulungu kuti atsikire pansi ndi kudzachita chinachake? Mwaona, uyu si munthu mmodzi yekha. Uwu ndi Mpingo wa Mulungu wamoyo, aliyense. Mukuona? Tsopano, aliyense akhale mu pemphero.

²⁵⁹ Tsopano, kodi ndi ichi? M'bale Banks, inu mungowabweretsa anthu azidutsa. Winawake ayime *apa*, ngati inu mungathe. Ali kuti mmodzi wa othandizirawo? M'bale Byrd, inu muwathandizire iwo azidutsa, ndiye. M'bale Banks, inu mubwere kuno, ndiye, ngati inu mungathe, kuno.

Tiyeni tipemphere.

Ambuye Yesu... [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]...?...

²⁶⁰ Inde, pitirizani kuwabweretsa iwo tsopano. Mulole iwo achiritsidwe, pamene ife tikuika manja pa iwo!...?...

Kazibwerani mtsogolo tsopano. Mmodzi aliyense wa inu, mupemphere tsopano!...?...

²⁶¹ Mu Dzina la Yesu Khristu...?... Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikuika manja...?...

Ndife okondwa kwambiri kuti...?... [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.]...?...

²⁶² Chiritsani odwala ndi osautsika, malo osiyanasiyana. Ndipo mulole iwo adalitsidwe, Atate, kwa ulemu ndi ulemelero wa Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

²⁶³ (Tsopano muwonetsetse...?... Ndiye mukhale okonzeka, apo pomwe?) Chabwino. Ngati...

²⁶⁴ Ambuye akudalitseni inu, m'bale. [M'bale akuti, "Ambuye akudalitseni inu. Ndine wochokera ku Sweet Home, Oregon, M'bale Branham."—Mkonzi.] Chabwino, kuchokera ku Oregon. ["Ndipo ife tidzakuwonani inu ku..."] San Jose. ["San Jose. Ife tikupita kumeneko."] Chabwino, zodabwitsa. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikuyembekeza—ine ndikuyembekeza kuti izo zidzangokhala umodzi wa misonkhano yaikulu kwambiri. ["Ifi tikudziwa izo zidzatero. Ngati Mulungu ali pamenepo, izo ziyenera kudzakhala."] Zikomo—zikomo—zikomo inu, m'bale wanga. Ambuye akudalitseni inu.

²⁶⁵ Kodi izi siziri monga Kumwamba? Pamene iwe uganizira, kulalikira Uthenga, ndipo miyoyo nkumakwezera manja awo kwa Khristu, odwala ndi osautsika akudutsa mu mzere, misonkhano ya ubatizo, chiyanjano, ubale, ndizo basi—pang'ono pokha Kumwamba kwagwera pansi pa dziko lapansi. Inu mukudziwa, ife... Ine ndikumverera monga zimene mtumwi ananena nthawi ija, "Ndi zabwino kuti ife tikhale pano." Ngati

ife tingakhoze . . . Ife sitikusowa koma Kachisi mmodzi. Koma ife timakonda kukhala pano kwa utumiki wa Mulungu.

²⁶⁶ Tsopano, aliyense wa anthu inu amene munabwera mu mzere mmawa uno, munapemphereredwa, ingokumbukirani, kuti Mulungu yemweyo amene wapereka zinthu zonse izi zimene mwamva kuti zikuchitidwa kuzungulira dzikoli, ndipo izo ndi zoonza, moona basi monga izo zingakhoze kukhalira. Ndipo atumiki onse awa pano, ndi zomwe zachitidwa mu utumiki wawo, zimene zachitika mu utumiki umene Ambuye wandipatsa ine, ife taima pano ndi kudzipereka, ndi mitima yathu yonse, tikupemphera, tikuika manja pa inu, ndendende basi zomwe Yesu ananena. “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzaika manja pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Tsopano izo zangokhala . . . Pali chinthu chimodzi chokha choti muzichiletsa kuti chisamachitike, icho chingakhale kusakhulupirira izo.

²⁶⁷ Yesu anati, “Idzani kwa Ine, inu nonse olema ndi othodwa, Ine ndidzakupatsani inu mpumulo. Aliyense amene akufuna, muloleni iye abwere.” Tsopano ilipo njira imodzi yokha yoti inu muziphonye izi. Mawu a Mulungu ndi owona. Njira imodzi yoti inu muziphonyere izi, si kubwera. Si kulondola uko? Ndi momwe inu mungaziphonyere izo.

²⁶⁸ Mulungu anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzaika manja pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Ilipo njira imodzi yokha yoti inu muziphonye izi, ndiyo kusazikhulupirira izo. Ngati mungakhulupirire Mawu a Mulungu, Mulungu adzasunga Mawu Ake. Inu mukuona, kwa . . . Izo zingakhale . . .

²⁶⁹ Ndiyo yoyamba, yoyambirira. Ndiyo njira yowapempherera odwala. Kuwadutsitsa iwo, kuyika manja pa iwo, kuwadzoza iwo, kapena chirichonse chimene Mulungu ananena, mwanjirayo. Koma kuwonjezera pa zonsezo, kuti Mulungu akudziwitseni inu kuti Iye ali pakati pa anthu Ake, Iye amasonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa. Ndipo, taonani, ndi zodabwitsa ndi zozizwitsa za Mulungu wamoyo, kuti azichita zinthu zimene Iye akuchitazi. Tsopano, Iye ndi wodabwitsa. Kodi inu simukuganiza chomwecho?

²⁷⁰ Tsopano abale akukonzekera, mmenemo, kwa—utumiki wa ubatizo. Ndipo izo zingokhala mofulumira. Ndipo tsopano, iwo amene ali oti abatizidwe, akazi apite ku chipinda. Nkulondola uko, akazi cha *uko*? Akazi cha *kuno*, ndi amuna mbali *iyi*.

²⁷¹ Pamene ife tikukonzekera utumiki wa ubatizo, Ine ndikufuna kuti ndiwerenge Lemba, mu maminiti pang’ono otsatirawa. Ndipo ife tidzakhala . . .

²⁷² Ine ndikudziwa kuti ina ya miyendo yanu iyenera kuti ikupweteka, chifukwa choimirira. Ndipo ngati inu mungakhoze kuimirira mphindi pang’ono chabe motalikirapo, inu muwona

mawonekedwe okongola pamene inu muziwona ku—kumizidwa kwa anthu awa.

²⁷³ Ine ndikufuna kuti ndiwerenge Malemba ena tsopano opezeka mu Bukhu la Machitidwe, mutu wa 2, pamene iwo akukonzekera ubatizo. Ine ndikuganiza pali pafupi awiri okha kapena atatu oti abatizidwe; sinditenga koma mphindi yokha. Ndipo ine ndikufuna kuti inu mumvetsetse mwatcheru tsopano. Ine ndiyamba kuwerenga kuchokera mu Machitidwe 2, ndime ya 28, kuyambira, kuwerenga.

Inu mwadziwitsa kwa ine njira ya moyo—njira za moyo (ziri mu zambiri); inu mudzandidzaza ndi chimwemwe ndi nkhope zanu.

Amuna ndi abale, ndiloleni ine ndiyankhule momasuka kwa inu za mbadwa Davide, kuti iye anafa ndipo anaikidwa, ndipo manda ake ali ndi ife mpaka tsiku lino.

Chotero pokhala mneneri, . . .

²⁷⁴ Ndi angati ankadziwa kuti Davide anali mneneri? Zedi. Iye anali wa salmo ndi mneneri.

Chotero pokhala mneneri, ndipo chidziwitso chimene Mulungu analumbirira ndi lumbari kwa iye, kuti mwa zipatso za m'chiuno mwake, monga mwa thupi, adzaukitsa Khristu kukhala pa mpando wachifumu wake;

Iye powona izi zisanachitike za chiwukitsiro cha Khristu, kuti solo yake siinali itasiyidwa mu hade, ngakhale mnofu wake sunawone chivundi.

Yesu uyu Mulungu wamuukitsa, chotero ndife tonse mboni zake.

²⁷⁵ Kodi zimenezo sizikumveka ngati lero? Ndife mboni za zinthu izi. Ine ndikhoza kunena, mmawa uno, “Hattie, nonse a inu, ndife mboni za zinthu izi.”

Chotero pokhala pa dzanja lamanja la Mulungu atakwezedwa; . . . atalandira kwa Atate lonjezo la Mzimu Woyera, iye wakhetsa ichi, chimene inu tsopano mukuchiwona ndi kuchimva.

Pakuti Davide sanakwere mmwamba: koma iye ananena iyemwini, AMBUYE anati kwa Ambuye wanga, Khala iwe pa dzanja langa lamanja.

²⁷⁶ Inu mukukumbukira Lamlungu lapitali momwe ife tinayankhulira za aneneri, amuna aakulu onse awo, momwe iwo ankayenera kuti afere? Koma Mmodzi anabwera, Mbewu yachifumu!

. . . Khala iwe pa dzanja langa lamanja,

Kufikira nditaika adani ako chopondapo mapazi ako.

Chotero lolani nyumba yonse ya Israeli idziwe ndithudi, kuti Mulungu wamupanga Yesu yemweyu, yemwe inu...munamupachika, ziwiri zonse Ambuye ndi Khristu.

Tsopano pamene iwo anamva izi (kuti Yesu anali ziwiri zonse Ambuye ndi Khristu); tsopano pamene iwo anamva izi, iwo analaswa mu mitima yawo, ndipo anati kwa Petro ndi...atumwi ena onsewo, Amuna ndi abale, ife tichite chiyani?

Ndiye Petro anati kwa iwo, Lapani, ndipo mubatizidwe aliyense wa inu mu Dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhululukiro cha tchimo, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.

Pakuti lonjezo liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo amene ali kutali, ngakhale onse amene Ambuye Mulungu wathu adzawaitana.

Ndipo ndi kuyankhula kwina kumene iye anachitira umboni ndi kulimbikitsa, kumati, Dzipulumutse wekha kwa m'badwo wopulukira uno.

Ndipo iwo amene mokondwera analandira mawu ake anabatizidwa: ndipo tsiku lomwelo kunawonjezeredwa kwa iwo pafupifupi miyoyo firii sauzande.

Ndipo iwo anapitirira mosakhazikika mu chiphunzitso cha atumwi ndi mu chijanjano, ndi... kunyema kwa mkate, ndi mapemphero.

Ndipo mantha anabwera pa moyo uliwonse: ndipo zodabwitsa zambiri ndi zizindikiro zinachitidwa ndi atumwi.

Ndipo onse amene anakhulupirira anasonkhana pamodzi, ndipo anali nazo zinthu zonse zofanana.

...anagulitsa chuma chawo ndi katundu, ndipo anawagawira iwo kwa anthu onse, monga munthu aliyense anali nako kusowa.

Ndipo iwo, mopitirira tsiku ndi tsiku ndi mgwirizano umodzi mu kachisi,...kunyema mkate nyumba ndi nyumba, anadya chakudya chawo mokondwera ndi mtima umodzi,

Kulemekeza Mulungu, ndi kukhala nacho chisomo ndi anthu onse. Ndipo Ambuye amawonjezera ku mpingo tsiku ndi tsiku monga iwo anapulumsidwira.

²⁷⁷ Tsopano basi pamene iwo akubwera ku madzi...Inu mundidziwitse ine pamene iye akufika, akupita ku madzi.

²⁷⁸ Kuti inu mukhoze kudziwa kuti chisomo cha pachokha chikulamulira ndi Mulungu, ine ndikufuna kuti ndibwerere. Ine basi sindingachitire mwina poyika chinachake mkatimo. Kodi

inu mumadziwa, anyamata awiri aja, ana a mkazi uja amene anapulumutsidwa, Mulungu anawadziwa iwo asanaikidwe maziko a dziko lapansi? Ndipo maina awo analembedwa kwenikweni pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa, asanaikidwe maziko a dziko lapansi. Baibulo limanena zimenezo. Ndipo izo zinkayenera kuti zigwire ntchito kwa miniti iyi.

²⁷⁹ Kodi inu mumadziwa, Mulungu anadziwa kuti ife tikanadzaima pano, zaka teni milioni dziko lisanakhazikitsidwe? Inu mukudziwa, Iye ankadziwa kuti ife tikanadzaima pano, mmawa uno. Kusapanda malire kwa Mulungu kunaidziwa ntchentche iliyonse, tongole aliyense, nthawi iliyonse izo zikanadzaphethira maso awo, ndi kuchuluka kwa zimafuta zowundana zikanadzatulutsa. Dziko lisanawumbidwe nkomwe, Mulungu ankadziwa zimenezo.

²⁸⁰ Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, ngati Iye amadziwa zimenezo, ndiye bwanji inu mukulalikira?”

²⁸¹ Ameneyo ndi Mulungu, gawo la dongosolo la Mulungu. Kulalikira ndiro dongosolo Lake. Pamene Iye anayang’ana pa atumwi...Iye anayang’ana pa zokolola. Iye anati, “Zokolola zacha, ndipo antchito ndi ochepa. Mupemphere Ambuye wa zokolola, kuti iye adzatumize antchito mu zokolola Zakezo.” Ndi angati akukumbukira zimenezo? Chabwino, nchifukwa chiyani iwo amayenera kupemphera kwa Ambuye wa zokolola, kuti atumize antchito mu zokolola Zake, ngati Ambuye wa zokolola anali ataima pamenepo, akudziwa kuti izo zikanachitidwa? Bwanji? Mulungu anzikonza izo motero, kuti Ake...Tsopano mveterani kwa izi. Mulungu anzikonza izo motero, kuti dongosolo Lake silingakhoze kuyenda popanda inu ndi ine. Ndipo bola ngati sitikuchita zomwe Mulungu akutitsogolera ife kuti tichite, ife tikulumalitsa dongosolo Lake. Koma pamene Mpingo usuntha mwa kudzoza kwa Mzimu Woyera, pamenepo ife tiri mu chifuniro cha Mulungu, tikuchita dongosolo Lake. Oh! Mwamsanga pamene ine ndidzabwerere kuchokera ku California, Ambuye akalola...

²⁸² Chimene Branham Tabernacle akusowa ndi chitsitsimutso. Ameni. Iwo akusowa chitsitsimutso ndi kudzadzidwa ndi Mzimu Woyera. Tsopano ndicho chosowa chachikulu cha kachisiyu. Ena a anthu abwino kwambiri mu dziko amabwera kuno, koma chimene ife tikusowa ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Ine ndikumverera izo, ndikhoza kudziwa izo. Ndipo mwamsanga ife tikadzabwerera, ngati Ambuye alola, ife tidzakhala ndi chitsitsimutso pa cholinga chomwecho, kuti mamembala a kachisi uyu, kumene anthu anali kufunafuna Mzimu Woyera, adzakhoze kubwera, adzalandire malangizo ndi china chirichonse. Misonkhano ya pemphero muno, kuti alandire Mzimu Woyera, kuti mpingo udzakhoze kubwerera mu chifuniro

cha Mulungu, ndi kumapitirira nalo dongosolo la Mulungu, pamene ilo likusunthabe chitsogolo.

Ambuye akudalitseni inu. Ine ndikukhulupirira iwo akonzeka tsopano pa dziwelo.

²⁸³ Inu mutenge izi, ndiyeno ine ndipita kumeneko ndi kukapemphera ndi iwo...?... 

59-1115 Utumiki Wanga Watsopano
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org